


KUTSIMIKIZIRA MAWU AKE

 Tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi chabe. Wokonededwa Atate Akumwamba, ndife oyamikira kuti tiri pano usikuuno. Ife, ife ndife oyamikira kuti tikudziwa Kukhalapo Kwanu kuli pano ndi ife. Tsopano ife tikupemphera kuti Inu mutumikire kwa aliyense wa ife, monga ife tiri ndi chosowa. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni. (Inu mukhale pansu.)

Ndikungomverera bwino kukhala ndi maikrofoni awa amoyo. Ine ndinali woepesa kwambiri kukhala ngati ndinawasokoneza iwo dzulo, Uthenga umene ine ndimafuna kuti inu muwumvetsere kwambiri.

² Ndipo ine ndimafuna kuti inu mukhale otsimikiza kuti muziwone izo. Ndi—nangula amene tiri naye. Ife sitinazikike ndi mpingo. Ife tinazikika mwa Khristu, inu mwaona. Iye ndi Njira yokhayo. Iye ndi malo okhawo otetezeka, malo okhawo amene Mulungu anayamba wayikapo Dzina Lake. Ndipo Mulungu anati Iye akanadzakumana ndi anthu mu malo amene Iye anawasankha kuti adzayikapo Dzina Lake; osati pa chipata chirichonse, koma pa chipata chimene Iye anachisankha. Ndipo mu malo amenewo Iye adzakomana ndi anthu, ndipo pamenepo pokha. Ndipo ife tikupeza kuti Mulungu sanayikepo Dzina Lake paliponse koma mwa Mwana Wake, Yesu Khristu, monga mwana nthawizonse amatenga dzina la bambo.

Ndipo tsopano inu mukuti, “Chabwino, kodi zimenezo zikugwira ntchito motani lero? Aliyense akuti, ‘Ine ndiri mwa Yesu.’”

³ Iye ndi Mawu. Kuti, “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Mawu anapangidwa thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.” Kenanso, izo zinalembedwanso mu Chivumbulutso mutu wa 19, pamene ife tinamuona Iye akubwera, Mkwatibwi ndi Mkwati, Chovala chake chinavikidwa mu Magazi, “Dzina Lake linatchedwa ‘Mawu a Mulungu.’” Iye ndi Mawu a Mulungu.

⁴ Ndipo, ndizo, Iye ndi mphamvu yofulumizitsa. Iye ndi Mzimu Woyera ndi kuti—mphamvu zimene zimabwera mu zimango, Mawu, zimene zimawapangitsa Iwo kukhala amoyo. Ndipo izo zonse zikuyenera kugwirira ntchito limodzi, kapena izo sizingagwire ntchito. Izo zikuyenera kutenga Baibulo lonse, Khristu yense, Uthenga wathunthu.

⁵ Ine ndikufuna kunena, kwa gulu ili limene ndinaliwonera pa televizioni usiku watha, podziwa kuti izo zichitika, ndipo ine ndinawonera izo. Ine ndikufuna kuwayikira ndemanga abale awa, omwe anali pa gulu limenelo, gawo loyankha

mafunso mwaluso chotero! Ndipo ine ndi wotsutsa kwambiri, inu mukudziwa, mulimonse, koma panalibe kanthu koti nditsutse pamenepo. Izo zinali zenizeni mwamtheradi, ndipo ine ndikanakhoza kuvomereza izo, handirede peresenti. [Osonkhana akuwombera mmanja—Mkonzi]. Zikomo inu. Amen. Mayankho amenewo anali olondola. Ine ndithudi ndinayamikira zimenezo. Ndimangolalakalaka ndikanakhala ndi filimu yoti ndikawonetse mu tchalitchi changa kwathu. Izo zinali zabwino kwenikweni.

⁶ Ndipo ndine wokondwa kwambiri kudziwa kuti—kuti Mulungu wachita mu madera enawo, pambali pa gulu lathu lomwe la Chipentekoste, ndipo akutengapo anthu, mbewu zimenezo za Mulungu, zimene zakhala ziri kumeneko zaka zonsezi, kudikirira Kuwala kuti kudzawalire pa iwo.

⁷ Ndipo zimatipatsanso ife chenjezo, abwenzi, kudziwa kuti Yesu anati, “Pamene namwali wogona uyu anadzayamba kubwera kudzagula Mafuta, apo ndi pamene Mkwati ankabwera.” Chotero ife tikhoza kuwona mwa izo, pamene ife tikuwona a Episcopalian, Presbateria Methodist, Baptist, Lutheran, akubwera kudzapeza Mafuta, ndiye limenelo linali ora limene Mkwati anadzabwera. Tiyeni tizikumbukira zimenezo.

⁸ Ine sindinakhalepo ndi Billy, mwana wanga, akunena zoterozo kwa ine monga iye anachitira mphindi zochepa zapitazo. Iye anati, “Adadi, ine sindimakuuzani inu choti muchite. Ine sindikufuna kukusangalatsani ndi chirichonse, koma,” anati, “adadi, chirichonse chimene inu mungachite, muziika nthawi yanu yonse kwa anthu odwala amenewo.” Iye anati, “Sindinawonapo odwala ambiri chotero!” Anati, “Ndinapereka makadi thuu handirede mu mphindi imodzi kapena ziwiri zokha.” Anati, “Pali anthu ambiri odwala!” Iye samandiuza konse ine zimenezo.

⁹ Ndipo kenako ine ndinabwera usikuuno ndi zolemba zina zazing’ono zolembedwa apa, ndi ndemanga zina pa chiweruzo chimene chikubwera, ndipo podziwa kuti ife takhala pano usikuuno ndi mkwiyo womwe wa Mulungu ukugwedezeka pansu pathu, ndipo posakhalitsa iye azigudubuza izo. Ndipo podziwa kuti mkwiyo wa Mulungu ukudikirira; pa nthawi imene izo zidzanenedwa, zidzakhala zitatha, kwa mamillioni. Ndipo podziwa izo mu mtima mwanga, ndi kudziwa izo kuti ziri chomwecho! Ndipo kenako ife tikuwona odwala ambiri, akukankhana ndi kukoka.

¹⁰ Ndipo ine ndinaganiza, “Usikuuno, ambiri a iwo ndi Akhristu.” Ndipo ndiroleni ine ndinene kwa ichi, inu ana a Mulungu. Chirichonse chimene mungachite, mulole china chirichonse chipite. Inu muzitumikira Mulungu, usana ndi usiku, ndi mtima wanu wonse. Inu, inu mukhoza kumverera kuti pali chinachake cholakwika. Mukhoza kuzindikira izo

pamene mukuyenda mmisewu, inu basi . . . ndi kulikonse kumene mungapite. Inu mukudziwa, ngati muli auzimu; ndipo ine ndikudziwa kuti muli.

¹¹ Ndipo ine ndinkayankhula ndi mwamuna, M'bale Stromei. Ine sindikudziwa ngati Tony ali pano, kapena ayi. Iye, iye anali . . . [M'bale akuti, “Tony Salameh?”—Mkonzi]. Tony Salameh, Salameh, Salameh? Ayi. Ine ndapeza Tony wolakwika. [M'bale akunena chinachake.] Ayi, ameneyo ndi Tony wolakwika. Uyu ndi Tony wa—wa—waku Tucson. Dzina lake ndi ndani? [Winawake akuti, “Stromei.”] Stromei! Ndikudziwa kuti ndi Salameh, Stromei, kapena china. Ndawapeza onse . . .

¹² Mu sitolo yake, tsiku lina, munabwera munthu, zinali zokhudza kwambiri, iye ankanena chinachake chimene chinabweretsa kukumbukira kwa ine, pamene ine . . . nthawi yomaliza imene ndinali ku—ku India.

¹³ Kumene, ine ndikuganiza Ambuye anatipatsa ife khamu lalikulu limene ife tinayamba takhalapo nalo pa nthawi imodzi, kunali ku Bombay. Ife sitinathe ngakhale kupeza malo owayikapo, ma teni amasauzande ndi masauzande a anthu.

¹⁴ Ndipo ife tisanafike kumeneko, apo panali nyuzipepala itamasuliridwa. Chabwino, ilo linali, India ndi dziko la zinenero ziwiri, inali—inali pepala ya Chingerezi. Ndipo anati, “Chabwino, zivomezi zikuyenera kuti zatha, mbalame zikuwuluka kubwerera kwawo ku zisa zawo.”

¹⁵ Masiku pang'ono chivomezi chisanafike, chimene chinagwetsa mipanda ndi zinthu. Mbalame zazing'ono zimadzipezera zokha mobisala mmathanthwe, ndi kumangamo zisa zawo; ndipo masana kapena pakati pa tsiku, pamene dzuwa likutentha kwenikweni, nyama zonse zimayima mozungulira makoma amiyala amenewo, kuti zilowe pamthunzi. Ndipo kwa masiku awiri, mbalame zinakhala mmitengo, izo sizinkapita ku zisa zawo; ndipo masiku awiri, ziweto, nkhosa ndi ng'ombe, izo sizinkabwera masana, kapena kukhala mozungulira makoma amenewo. Izo—izo zinakakhala kunjira mmunda ndipo nkutsamirana ina ndi imzake, pofuna mthunzi.

¹⁶ Ndiye zonse mwakamodzi, chivomezi, chimene chinangogwedeza makoma ndi kugwetsera pansi nyumba. Ndipo, mwaona, ngati mbalame zazing'ono zimenezo zikanakhala mmenemo, izo zikanawonongeka. Ngati ng'ombe zikanakhala zitaima pansi pake, ndi nkhosa, izo zikanawonongeka. Mulungu akuchenjeza chirengedwe!

¹⁷ Masiku angapo apitawo, uko mu sitolo ya M'bale Tony, ine ndinali kumumvetsera mwamuna kumeneko amene ankanena . . . Pamene chivomezi ichi chinachitika mu Alaska, iye anali akuwedza uko mu chimene ife timachitcha Stony Point, ku Mexico. Ndipo iye anati, “Mbalame sizinkadya, ndipo

nsomba sizinkadya. Panali chinachake cholakwika. Ndipo, zonse mwakamodzi, chivomezicho chinayamba.”

¹⁸ Ndipo tsiku lina, pamene icho chinachitika uko ku India, kapena kulikonse kumene icho chinali, iye anati iye ankawedza kenanso. Iye anaganiza, “Chabwino, izo ndi zachirendo. Nsombazo zimadya pafupifupi nthawi iyi. Mulibe mpukutu mmadzi, paliponse. Madziwo angokhala chete, nthawi yabwino yoti nsomba zidye, koma izo sizinadye. Ndipo mbalame zonse zimene kawirikawiri zimakhala kunjira uko, mbalame za kauye, zikutola nsomba izi ndi zinthu, zonse zinkayenda pa gombe, zitatsamirana wina ndi mzake. Mu kamphindi pang’ono, ndere za mnyanja kuchokera pansi zinayamba kukwera monga *choncho*, chivomezi chinachitika kutsidya lina la dziko lapansi.” Mwaona, nsombazo zinkadziwa kuti panali chinachake cholakwika, chinachake chinali pafupi kuchitika. Mbalamezo zinkadziwanso chimodzimodzi.

¹⁹ Ndithudi, ngati Mulungu amayipatsa nsomba ndi mbalame kuzindikira, ndi zochuluka bwanji kuti Iye apereke kwa Ake—ana Ake! Iye tikudziwa kuti ife tiri ku mapeto a nthawi, ndipo chiweruzo chikuyembekezera, chotero tiyeni tikhale olemekesa kwenikweni. Thawirani kwa Mulungu ndi mtima wanu wonse! “O Kaperna, iwe amene wakwezedwa kumwamba, udzatsitsidwira ku gehena,” ndipo lero iye akugona pansi pa madzi. Muzingokumbukira, ndi kumapemphera.

²⁰ Tsopano, usikuuno, ndikufuna kuti ndiwerenge malo apa mu Lemba, kwa mphindi pang’ono chabe. Iye tipempherera odwala. Billy anati iye anapereka mulu wa makadi apemphero. Ndipo iye anapereka ena dzulo, ndipo ine sindinafikire kwa aliwonse a iwo usiku watha. Ndipo ine ndinadabwa, pamene Mzimu Woyera unabwera...Ndipo basi...Inu simungakhoze kuwupanga Iwo kugwira ntchito. Ziri ngati chogwirira chaching’ono, mumadzikokera nokha mu giya. Ndinu amene mumagwira ntchito ya Mzimu Woyera, osati ine. Inu mumachita zimenezo nokha. Chotero ine, usiku watha, ine ndinazindikira ngakhale mu kuzindikira za mumtima, izo sizinagwirizane konse ndi anthu molondola basi. Iwo samawoneka kuti akuzitengera kwa izo. Ine ndazipeza izo, apa posachedwapa, zikuwoneka ngati, mochulukirapo kapena mochepera, basi pamene ine ndinali kuyankhula, kusanjika manja pa odwala, iwo akudziwa.

²¹ Iye tikuyenera kuzindikira kuti mwa ife mwapatsidwa, ife amene timakhulupirira Yesu Khristu ndipo tinabadwa mwa Mzimu Wake ndi kudzazidwa ndi mphamvu yofulumizitsa imeneyo, mphamvu imeneyo imene ili mwa inu. Ndi kusanjika manja, pa ena, monga ophunzira anachitira, ndi kudutsa kupyola mu m’badwo, Iwo mwamtheradi unachiritisa odwala, unawukitsa akufa, Iwo unasonyeza masomphenya, maulosi. Ndipo Mzimu womwewo umene unakhala pakati pa atumwi oyambirira ukukhala mu mpingo lero, ukugwira ntchito zinthu

zomwezo. Ndipo mwamsanga momwe ife tingathere kuzindikira izo! Mwaona, ziribe kanthu momwe izo zikugwirira ntchito, inu mukuyenera kuzindikira zimenezo ndi kuzikhulupirira izo. Izo sizingachite ubwino uliwonse, mpaka inu mutakhulupirira izo. Koma pamene inu mukukhulupirira izo, mavuto anu atha. Izo nzoona.

²² Tsopano tiyeni ife titembenukire mu Lemba. Ine ndinali nditakhala kunja uko, mphindi zingapo zapitazo, ndinalimba Malemba ena angapo, kuti ndisintho mutu wanga wa usikuuno. Ndipo ine ndikufuna kuti ndiwerenge zina kuchokera mu Mawu a Mulungu, kuchokera mu Bukhu la Luka Woyera, mutu wa 8, kuyambira ndime ya 40. Mvetserani tsopano, ine ndiwerenga motalika.

Ndipo kunali, kuti, pamene Yesu anadza, anthu ambiri anamulandira iye mokondwera: pakuti onse ankamudikirira iye.

Kodi izo sizingakhale mawonedwe abwino kwa gululi usikuuno?

Ndipo, taonani, anadza munthu dzina lake Yairo, ndipo iye anali mkulu wa sunagoge: ndipo anagwa panso pa mapazi a Yesu, ndipo anamupempha iye kuti apite ku nyumba yake:

Pakuti iye anali ndi mwana wamkazi mmodzi yekha, wa pafupifupi usinkhu wa zaka thwelofu, ndipo iye anali akufa. Koma pamene iye ankapita anthu anamuunjikira iye.

Ndipo mkazi wa vuto la magazi zaka thwelofu, amene anawononga zonse za moyo wake kwa asing'anga, ndipo sanakhoze kuchiritsidwa ndi aliyense,

Anabwera pambuyo pake, ndipo anagwira mphonje ya chovala chake: ndipo pomwepo vuto la magazi lake linatha.

Ndipo Yesu anati, Ndani wandikhudza ine? Pamene onse anakana, Petro ndi iwo amene anali ndi iye anati, Mphunzitsi, khamu la anthu likukukankhani inu ndi kukupanikizani inu, ndipo inu mukuti, Ndani wandikhudza ine?

...Yesu anati, Wina wandikhudza ine: chifukwa ndazindikira kuti mphamvu yachoka kwa ine.

Ndipo pamene mkaziyo anawona kuti sanabisike, iye anabwera akunjenjemera, ndipo anadzagwa panso pamaso pake, ndipo anafotokoza kwa iye pamaso pa anthu onse chifukwa chimene anamukhudzira iye, ndi momwe iye anachiritsidwira pomwepo.

Ndipo anati kwa iye, Mwana wamkazi, limba mtima: chikhulupiriro chako chakuchiritsa iwe; pita mu mtendere.

Ndipo pamene iye... ankayankhula, anadza munthu wina wochokera kunyumba ya mkulu wa sunagoge, nanena naye, Mwana wako wamkazi wafa; usamuvutitse Mphunzitsi.

Koma pamene Yesu anamva izo, iye anamuyankha iye, kuti, Usawope ayi: khulupirira kokha, ndipo iye achiritsidwa.

Ndipo pamene iye analowa mnyumba, iye sanaloleze munthu kulowa, kupatula Petro, ... Yakobo, ndi Yohane, ndi atate ndi amayi a namwaliyo.

Ndipo onse analira, . . . anamulira iye: ndipo iye anati, Musalire ayi; iye sanafe, koma wagona.

Ndipo iwo anamuseka iye monyoza, podziwa kuti iye anali atafa.

Koma Iye anawaturutsira onse panja, ndipo anamugwira iye dzanja, ndipo anayitana buthulo, nanena, Buthu, dzuka.

Ndipo mzimu wake unabweranso, ndipo iye anawuka pomwepo: ndipo analamula kuti amupatse iye nyama.

Ndipo makolo ake anazizwa: koma iye anawalamula iwo kuti asamuuze munthu aliyense chimene chinachitika.

²³ Tsopano tiyeni tipemphere. Okonedwa Atate Akumwamba, pamene tikuwerenga Mawu awa, ife tikudziwa kuti icho ndi choonadi. Ichi chinachitika. Iyi si nkhani yopeka imene tingawerenge kuchokera mu nyuzipepala kapena bukhu lina la nthano, koma iyi ikuchokera mu Bukhu limene ife tikulidziwa kuti ndi Mawu a Mulungu. Ife tikukhulupirira izo zinachitika. Ife tikukhulupirira kuti Yesu uyu amene anachita chinthu chodziwika ichi, nthawi ziwiri apa, cha mkazi wa nthenda ya magari, ndi mwana wakufayo, ife tikukhulupirira kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu, kuti Mulungu anamuukitsa Iye kwa akufa ndipo wamupereka Iye kwa ife, usikuuno, mu umunthu wa Mzimu Woyera.

²⁴ Ndipo ife tikukhulupirira kuti Iye ali pano ndi ife usikuuno. Ndipo kukhulupirira kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, chifundo Chake chimafikira kwa anthu. Ndipo pamene anthu akufikira kwa Iye, zotsatira zomwezo zimene zinaperekedwa mu tsiku limenelo ziperekedwa lero. Perekani izi kenanso, Atate, kuti ife tithe kukhala ndi kudzoza kwatsopano. Monga M'bale Shakarian anapempha moona mtima, kanthawi kapitako, ndipo anapempha omvera kuti akhulupirire, ife tikupempha kenanso mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

²⁵ Ine ndikufuna kuti ndiyankhule kwa mphindi zochepa chabe, ndipo izo zikhala mphindi zochepa chabe, chifukwa ine ndikufuna kuti ndiwatengere anthu awo kuno amene ali ndi makadi apemphero ndi kudzawapempherera iwo. Ndi kusiya chinthu china chirichonse koma kumangopempherera odwala. Koma ife tisanapempherere odwala, ife tikuyenera kuwatengera anthu mu chikhalidwe chimenecho. Ndi khalidwe limene nthawizonse limabweretsa zotsatira. Ndi khalidwe limene mumalitengera kwa Mulungu.

²⁶ Apa pali mkazi anagwira chovala Chake, iye anachiritsidwa, ndi vuto la magazi. Msilikari anamulavulira pa nkhope Yake ndipo anamuveka chisoti chaminga pa mutu Wake, ndipo sanamverere ukoma.

²⁷ Ndi mafikidwe anu. Khalidwe ndi limene limapanga izo. Ndipo ndi zomwe ziri usikuuno, mzanga wokondedwa, zimatengera khalidwe. Ife tiri, ndipo tikukhulupirira kuti ife tiri, mu Kukhalapo kwa Yesu Khristu, koma ndi khalidwe lanu limene limabweretsa zotsatira. Zimango ziri pano, ndiponso mphamvu. Ngati mutangoyamba, Mulungu adzachita zina zonsezo.

²⁸ Tsopano, phunziro ili limene ine ndikufuna kuti ndiyankhulepo, kwa mphindi pang’ono, ndi: *Kutsimikizira Mawu Ake*. Tsopano icho ndi chinthu chachikulu, kuganiza za zimenezo: *Kutsimikizira Mawu Ake*.

²⁹ Tsopano Mulungu ndi wokhoza basi kutsimikizira Mawu Ake, usikuuno, monga Iye ankawatsimikizira Iwo nthawizonse. Ndipo Baibulo nalonso linati, “Tsimikizirani zinthu zonse. Gwiritsitsani kwa icho chimene chiri chabwino.”

³⁰ Tsopano inu mwamvapo, mosakayikira, munamvapo mwambi wakale, “Tsimikizirani izo, ine ndikhulupirira izo.” Koma izo sizikhala zooni. Nthawi zambiri ine ndawonapo zinthu zambiri zikutsimikiziridwa, zimene zinali mwamtheradi zotsimikiziridwa mwasayansi, ndipo komabe anthu samakhulupirira izo mulimonse.

³¹ Ine ndimayankhula ndi munthu, kuno osati kale kwambiri. Ife tinali kuyankhula za machiritso Auzimu. Iye anati, “Ine sindingakhulupirire izo. Ine sindikusamala chimene chingachitike, umboni wochuluka bwanji umene inu mungawonetse pa izo, ine sindikhulupirirabe izo.” Chabwino, ndithudi, ziribe kanthu chimene inu mungamuchitire munthu ameneyo, iye—iye watayika. Iye sangakhulupirire. Mulibemo kalikonse mwa iye, kuti akhulupirire.

³² Ndinangokhala ndi a—chondichitikirira chaching’ono apa, pafupifupi sabata yapitayo, monga inu nonse mukudziwira kuti ine—ine ndimasaka. Ndipo pamene ine ndinabwerera kuchokera ku msonkhano wanga, ine ndinakhala ndikusaka mikango. Ndipo ine nditasamukira ku Arizona, nzabwino, ine

ndimakonda kusaka nyama zazikulu, ndipo ine ndimakonda kupita kunja pakati pa chirengedwe ndi kumakachiyang'ana icho.

³³ Tsopano, ine sindine wakupha. Ine ndimangosaka. Chotero, ine—ine sindimakonda kuwononga ziweto, ine—sindikuganiza kuti izo ndi zolondola. Ine ndikuganiza kuti ndi tchimo lochuluka kupha nyama, pamene sukuigwiritsa ntchito ndi kugwiritsa ntchito kwa cholinga, monga zingakhalire kupha china chirichonse. Ine ndikukhulupirira kuti ndizolakwika. Iye sitikuyenera kumachita zimenezo. Mulungu anapereka izo kwa ife ngati chakudya ndi zolinga zake, ndipo sitikuyenera kumaziwononga izo. Koma tsopano zimene lamulo linena inu mukhoza kutenga, chabwino. Musamangoziwononga izo.

³⁴ Ndipo ine kumusi uko, nyengo yatha kwa china chirichonse. Mikango imapha ng'ombe zambiri. Ndipo ndikuwadziwa oweta ambiri mu dziko muno. Ndipo nthawi iliyonse iwo akapha, bwanji, iwo amandiitana ine, pamene mkango ufika pakati pa nkhusa. Mzanga wina, usiku wina, anataya pafupifupi madola sarte faivi handirede, mu usiku umodzi, ndi mkango umodzi utapha ana ankhusa okha. Iye analowa, ndipo, ndithudi, mikango yotsalayo iyenera kulipira chifukwa cha tchimo lake. Ndipo chotero ine ndinawupeza mkangowo, ndipo chotero iwo unali mkango wawukulu kwambiri, ndi kutalika kwa mapazi naini, ndipo unkalempera pafupifupi thuu-chakuti, chotero iwo unali—unali mkango waukulu wabwino.

³⁵ Ndipo kenako ine ndinapita kuchokera ku dziko la Arizona, kupita ku Utah, kukasaka. Ndipo chotero ine ndinauzidwa kuti kunali anthu kumtunda uko, kuti mwamuna yemwe ine ndimati ndikasaka naye, anali wotchera misampha wa boma, “Ndipo, chifukwa cha ubwino, musatchule chirichonse chokhudza chipembedzo, mozungulira iye.” Anati, “Iye analidi munthu waukali.”

Ndipo ine ndinati, chabwino, ine ndinamuuza mwamuna amene ine ndinkapita naye, ine ndinati, “Ine sinditchula izo.”

³⁶ Iye anati, “Usanene 'mlaliki.' Ngati iwe utero, sudzafika konse kokasaka. Iye sadzakutangani inu.” Anati, “Ine ndinasaka naye iye masiku atatu, ndipo ndimagona naye usiku uliwonse, kudya naye tsiku lililonse, ndipo sananene nkomwe, 'Mmawa wabwino. Inu muli bwanji? Mukufuna chinachake choti mudye? Tsuka mbale.' Palibe!” Anati, “Tsopano musanene kanthu za izo.”

Ine ndinati, “Ine sindinena mawu.” Chotero sindinamuuze iye kuti sindingapemphere, koma ndinangopitiriza kumuuza iye kuti ine ndi . . . Ndipo ine ndikupemphera.

³⁷ Chotero pamene tinakafika kumeneko, mwamunayo anali munthu wowuma mtima kwambiri, ndipo sindinaganize kuti iye ankakhulupirira chirichonse. Ndipo iye anali atangotaya

kumene khanda mausiku angapo izo zisanachitike, khanda lobadwa lakufa. Chotero, ife tinapita kukasaka. Ndipo pa tsiku lachiwiri, mwamuna amene ine ndinkasaka naye anali atamuuya iye, anati ine ndikhoza kusaka kulikonse kuzungulira dzikolo. Chotero pamene mlenje winayo, anali ndi ine, anachokapo, ife tinali pamwamba pa nsonga; kumene ife tinangothamangitsa mkango, mpaka ife tinaufikitsa iwo mu miyala, ndipo iwo unali utathawa. Ndipo chotero ife tinali titakhala pamenepo kudikirira kuti galu abwerere. Ndipo munthu uyu ananena kwa ine, iye anati, “Mlenje winayo, mzakoyo, amandiuza ine kuti inu mumasaka kulikonse. Kodi muli ndi ndalama zambiri?” Anati, “Ndikuganiza izo si ntchito yanga.”

Ndipo ine ndinati, “Ayi,” ine ndinati, “si ndalama zambiri.” Ine ndinati, “Ine—ine ndimathandizidwa.”

Ndipo iye anati, “Oh, ndawona.” Iye anati, “Chabwino, ndikuganiza kuti si ntchito yanganso, koma,” anati, “kodi muli mu gulu limene limakuthandizani?”

Iye ankachikoka icho kuchoka mwa ine. Ine ndinalonjeza kuti sindizatero, mwaona. Chotero ine ndinati, eya, ine ndinati, “Ayi, bwana. Ndine mlaliki, wa misionare.”

Iye anati, “Ndi chiyani?”

Ine ndinati, “Mmisionare.” Ndipo iye anangoyima ndi kumandiyang’ana ine kwa maminiti pang’ono.

Ine ndinati, “Kodi iwe uli ndi chiyembekezo chirichonse cha Moyo tikadzachoka kuno? Chiyembekezo chako ndi chiyani?”

Iye anati, “Ndine wa Jack Mormon.”

Ndipo ine ndinati, “Wa chiyani?”

Iye anati, “Wa Jack Mormon.”

Ine ndinati, “Ndi mtundu wanji umenewo?”

Anati, “Amene amatukwana ndi kumwa khofi, ndi kusuta ndudu.”

Ine ndinati, “Chabwino, kuvomereza kowona mtima ndi kwabwino ku moyo.”

³⁸ Ndipo kenako iye anati—iye anati, “Ine ndikufuna ndikufunsemi inu chinachake.” Iye anati, “Ndauzidwa kuti mpingo wa Mormon ndi mpingo woota wokhawo umene ulipo.” Iye anati, “Kodi mumakhulupirira zimenezo?”

³⁹ Ine ndinati, “Zikafika ku mpingo, ndikuganiza kuti ndi wabwino ngati uliwonse wa iyo. Ine ndimadziwa Choonadi chimodzi chokha, ndipo ndicho Yesu Khristu.” Ine ndinati, “Ine ndikudziwa Iye ndi Woota.”

⁴⁰ “Chabwino,” iye anati, “Ine ndinali ndi mwana atabadwa usiku wina, anabadwa wakufa.” Iye anati, “Ine ndinauzidwa kuti mwana uyu, chifukwa iye anabadwa wakufa, Mulungu sanauzire

konse mpweya wa moyo mwa iye, kuti ine sindidzamuwonanso iye kenanso.” Iye anati, “Inu mukuganiza chiyani za zimenezo?”

⁴¹ “Chabwino,” Ine ndinati, “Iwe sudzatero ngati wa Jack Mormon, iwe ndithudi sudzatero. Ndi chinthu chimodzi chotsimikizika, iwe sudzamuwona iye ngati ungakhale wa Jack Mormon.” Ndipo iye anati . . . Chabwino, iye anali akundikankha ine, chotero ine ndinamukankhira iye mmbuyo pang’ono pokha, inu mwaona. Ife tinali—tinali ndi nthawi yokankhira mmbuyo. Chotero iye anati—iye anati . . . Ine ndinati, “Vuto ndi chiyani?”

Iye anati, “Oh, ine sindikudziwa.” Ndipo anati, “Chabwino, inu mukuganiza chiyani?”

Ine ndinati, “Ine ndikudziwana ndi ambiri abwino . . .”

⁴² Ine sindinkadziwa kuti iye anali wa Mormon. Ndipo ine ndinali kwambiri . . . Ine ndikudziwa, pokhala ku Utah, mwina zinali, koma ine . . . chifukwa anthu ambiri kumeneko ndi a Mormon, kuzungulira Salt Lake City. Iyi sinali Salt Lake City, komabe. Chotero ine ndinaganiza, “Chabwino, ine ndakhala nawo abwenzi abwino achi Mormon, akhala ali mu mizere ya pemphero, anthu abwino.”

⁴³ Ndipo ine ndinati, “Ndakumana nawo amuna abwino kwambiri amene ndi—ndi a Mormon.” Ndipo iye anati, chabwino, iye anati . . . ine ndinati, “Sindichidziwa chiphunzitso chawo pa izo, ndipo ine sindikanafuna kunena chinachake chosiyana ndi chiphunzitso chawo, chifukwa ndi chimene inu muli, ndipo ine ndimalemekeza izo kwambiri.” Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ndipo inu mukukhulupirira zimenezo?”

Iye anati, “Inde, bwana, ndikutero. Koma,” anati, “Ine sindimakhala moyo kwa izo.”

⁴⁴ Ine ndinati, “Chabwino, ine ndikukhulupirira kuti Baibulo limaphunzitsa kuti Mulungu ankamudziwa mwana ameneyo, mamillioni a zaka zapitazo, maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe.” Ine ndinati, “Mulungu anamuza Yeremiya, ‘Usanalengedwe mmimba mwa amayi ako, usanatuluke konse kuchokera mmimba, Ine ndinakudziwa iwe, ndinakuyeretsa iwe, ndipo ndinakudzoza iwe mneneri wa mafuko.’” Ine ndinati, “Umo ndi momwe Iye ankadziwira za izo, mwaona.”

Iye anati, “Chabwino,” iye anati, “zikomo.”

⁴⁵ Iye anayamba kuyenda motsika phirilo. Ndipo kenako iye anakumana ndi munthu wina uyu, ndipo iye anati, “Chifukwa chiyani iwe sunandiuze kuti munthu ameneyo ndi mlaliki?” Ndipo chotero ife . . . Iye anayankhula naye pang’ono ndipo anayamba kumuza iye za misonkhano.

⁴⁶ Tsopano, a Mormon amakhulupirira uneneri. Ine sindi . . . mwina mulibemo aliwonse muno, koma iwo—koma iwo amakhulupirira mu—mu uneneri. Koma, chotero, mwinamwake

ine ndikuyankhula kunja kwa sukulu, koma ine...Eya. Eya. Koma, komabe, iwo amakhulupirira.

Ndipo iye anati, iye anabwerera kwa ine, anati, “Ndamva kuti ndinu mneneri.”

Ine ndinati, “Ayi, bwana.” Ine ndinati, “Ine...Ambuye andiwonetsapo zinthu zingapo zoti zichitika.”

⁴⁷ Ndipo ananyamuka, nthawi yomweyo, anati, “Tiyeni tilowe.” Ndipo iye analowa mu galimoto yake, ndipo anapita kumusi ku...mzinda wake waung’ono kumene ankakhala. Mu kanthawi kochepe, iye anadzasowa. Ife tinkakonza agalu, kuti tikasakenso titadya chakudya chamasana. Ndipo pamene ife tinatero, bwanji, iye ananyamuka mu galimoto.

⁴⁸ Mu mphindi zochepe, mnyamata wowoneka bwino anabwerera, pafupifupi usinkhu wa zaka seventini, njonda yeniyeni yowoneka-yoyera ya Chikhristu. Iye anati, “Uyu ndi mchimwene wanga.” Anati, “Iye si wa Jack Mormon. Iye ndi Mormon weniweni.”

Ine ndinati, “Uli bwanji, mnyamata?”

Ndipo iye anati, “Ine ndamva, kuti mchimwene wanga amandiuza ine, kuti inu ndi mneneri.”

Ine ndinati, “Ayi, bwana.” Ine ndinati, “Sikuti ndine mneneri.” Ine ndinati, “Ambuye wandiwonetsapo zinthu zoti zichitika.”

⁴⁹ Iye anati, “Ine ndiri ndi chipolopolo mmanja mwanga pakali pano, ndikuyenera kukakhala pa tebulo la opareshoni.” Iye anati, “Koma mchimwene wanga wandiuza ine izi. Ndipo ine ndinati, ‘Ngati ziri chomwecho, ine sindikusowekera opareshoni.’” Iye anadzandiyang’ana ine cholunjika mmaso, kowona mtima, kuyang’ana, kowona, kodzipereka, anati, “Inu muyiike manja anu pa ine. Ngati zinthu izi ziri choncho, sindisowekera opareshoni.” Iye anapita kwawo ali bwino.

⁵⁰ M’bale uyu, mzanga wa Chikhristu, ankasaka ndi ine, wochokera ku Phoenix. Iye anati kwa ine, iye anati... Ena a anyamata awa akhala pano tspano. Mmodzi wa iwo amene ndikumudziwa ali pano. Ife tinapita kunyumba. Iye anati, “M’bale Branham, ngati Ambuye angakuwonetseni inu masomphenya ndipo ndikukulolani inu muwawuze a Mormon amenewo basi chimene chiti chichitike, icho chidzachita icho, chifukwa iwo akufunafuna icho.”

⁵¹ Chotero, ine ndinapemphera ndipo ndinapemphera. Ndipo pa ulendo wanga wobwerera kwathu, ine ndinali kubwera, Lolemba lotsatira, Lamlungu, pafupifupi teni koloko, ine ndinali nditayima mchipindamo, titachoka ku tchalitchi mmawa umenewo, ndipo ndinkayang’ana panja.

⁵² Ndipo ine ndinawona magetsi akuthwanima, kapena mtundu wina wa kuwala ukuthwanima. Ndipo ine ndinawona

mkango umene unali mu mtengo, ndipo—ndipo unali waung’ono kwambiri kuti ndiwuwombere. Ine sindinawufune iwo. Ndipo panali winawake anawombera iwo, ndipo, pamene iwo anatero, iwo anawuwombera iwo ndi mfuti yaikulu kwambiri. Iyo inawuphulitsa mkangowo. Ine sindinayamikire a—a—momwe izo zinachitikira.

⁵³ Pamene ine ndinafika ku Phoenix, ine ndinamuuzza M’bale Dawson zimenezo, ndi M’bale Mosley. Ine ndikudziwa kuti iye ali pano. Ine ndinamuwona iye tsiku lina, penapake kuno. Ndipo iye ankakwera ndi ine, iye ndi mkazi wake. Ndipo ine ndinati, “Inu tayang’anani ndipo muwone, ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Izo zichitika mwanjira imeneyo.”

⁵⁴ Mausiku ife tinadikirira, mausiku anayi kapena asanu, ife tinali titasaka, kapena masiku. Kawirikawiri mkango sumakwera mu mtengo usiku. Zinachitika kuti, akubwera kunyumba, iwo anawamasula agalu, mlenje uyu, mnyamata wachi Mormon uyu. Ndipo a—mkango unadzagunda kanjira, kapena galu anadzagunda kanjira ka mkango, kani, ndipo anawuthamangitsira iwo mu mtengo. Ndipo pa teni koloko usiku iwo anabwera, anadzatidzutsa ife. Ife tinapita kunja uko, ndipo uko kunali mkango womwewo mu mtengo. Ukuthwanimitsa nyali, M’bale Mosley anawuwombera iwo ndi mfuti ya mtundu wa forte-foro, anakhala ngati awuphulitsa mkangowo pawiri. Ndipo apo izo zinali, ndendende basi momwe izo zinanenedwera.

Tsiku lotsatira, ndinakumana ndi woyang’anira zinyama wa bomalo, Jack Mormon wina. Ndinawatenga anyamata amenewo pamodzi, kuwatsogolera iwo kubwerera kwawo kwa Khristu.

Ine ndikukuuzani inu, Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Mulungu amatsimikizira Mawu Ake kuti ali chomwecho.

Inu mwamvapo anthu akunena kuti, “Kuwona ndi kukhulupirira.” Izo sizowona konse. Anthu ambiri amawona ndipo samakhulupirirabe.

⁵⁵ Masiku amene Yesu anali pa dziko lapansi, bwanji iwo sanamuzindikire Iye, kuti Iye anali Mawu a Mulungu aja atawoneteredwa? Nchifukwa chiyani anthu sanazindikire kuti Mose anati, “Yehova Mulungu wanu adzadzutsa mneneri wonga ine”? Ndipo Iye anakwaniritsa Mawu aliwonse amene Baibulo linanena kuti Iye akanati adzachite, koma iwo sanakhulupirire izo.

⁵⁶ Koma Mulungu, mu m’badwo uliwonse, amatsimikizira Mawu Ake kuti ndi owona. Iye nthawizonse amatsimikizira Mawu Ake. Ndiye nthawizina iwo amati, “Kuwona ndi kukhulupirira.” Izo si choncho. Koma ife tikudziwa kuti Mulungu amapitirirabe kutsimikizira Mawu Ake mu m’badwo uliwonse.

57 Ife timadziwa kuti Iye anatsimikizira izo kwa Adamu ndi Eva, kuti pamene Iye anati, “Tsiku limene inu mudzadya za iwo, tsiku limenelo inu mudzafa ndithu.” Ife tikuyenera kuvomereza kwa izo, kuti izo nzoona. Ife timakhulupirira izo, pakuti Iye wazitsimikizira izo kwa ife, ndipo ife tikudziwa kuti izo ndi choonadi.

58 Tsopano ife tingotenga malo ena amene Mulungu anatsimikizira Mawu Ake. Tiyeni titenge, mwachitsanzo, mu masiku a—a Nowa. Mulungu anayankhula kwa Nowa uthenga wosagwirizana ndi sayansi komanso wosakhulupiririka. Palibe amene akanakhulupirira. Kunali kusanagwepo mvula pa dziko lapansi. Zosagwirizana ndi sayansi!

59 Mwinamwake iwo unali m’badwo wopambanako wasayansi nthawi imeneyo kuposa momwe ife tiriri tsopano, chifukwa iwo ankamanga mapiramidi ndi masifinki, ndi zina zotero, mmasiku amenewo, zimene ife sitingazimange tsopano. Iwo ankaidziwa mphamvu, ya mtundu wina wa mphamvu yamakina, mwinamwake ya atomiki kapena chinachake, kuti iwo ankakhoza kukweza matanthwe aakulu amenewo, amene ife sitingathe kuchita izo lero. Koma iwo ankachita zinthu zazikulu za sayansi. Iwo anali ndi chinachake chimene ankatha kukonza mtembo, kuti uwoneke mwachibadwa kwa zaka mahandirede. Ife tinataya luso limenelo.

60 Yesu anati, “Monga zinaliri mmasiku a Nowa, zidzakhalanso choncho pa kudza kwa Mwana wa munthu.” Ndipo ife tikudziwa kuti ife tikuyenera kulowa mu m’badwo wina waukulu wa sayansi.

61 Ndipo tsopano uthenga umene Nowa anali nawo unali wosiyana kwambiri ndi chikhulupiro cha tsiku limenelo, mu mpingo, ndipo iwo unalinso wosiyana kwambiri ndi kafukufuku wa sayansi. Koma Mulungu anatsimikizira Mawu Ake kukhala choonadi. Mulungu anatsimikizira kuti chimene mneneriyo ananena chinali choonadi.

62 Komanso titenga wina kwa mphindi chabe. Abrahamu anali mneneri wina wa Ambuye, amene Mawu anabwera kwa iye. Ndipo anamuza iye, pamene iye anali wa usinkhu wa zaka sevente-faivi, ndipo Sarah anali wa usinkhu wa zaka sikisite-faivi, kuti iye adzakhala ndi mwana mwa Sarah. Tsopano, icho chinali chodzidzimutsa kwambiri kwa wosakhulupirira. Kodi inu mungaganizire, lero, chinthu choterocho chikuchitika ngakhale lero, ndi zopambana zathu zonse zasayansi, ndi ana onse a mmachubu oyesera awa amene iwo amawakamba, ndi zina zotero? Koma mkazi wokalamba uyu, tsopano wa usinkhu wa zaka sikisite-faivi, ndi nkhalamba ya usinkhu wa zaka sevente-faivi, koma Mawu a Ambuye anabwera kwa Abrahamu ndipo anamuza iye kuti izi zikanadzachitika. Ndipo Abrahamu anakhulupirira Mulungu. Tsopano, ziribe kanthu ndi mochuluka

bwanji momwe Mulungu anayankhulira, ndi momwe izo zinali zoono, Abrahamu ankayenera kukhulupirira chimene Mulungu ananena, kuti achipange icho kukhala chomwecho. Tsopano onani momwe munthu uja anayesedwa, ndi umboni wake, kuti iye anakhulupirira.

⁶³ Munthu yemweyo amene anapanga kuvomereza kumeneko, kuti iye anakhulupirira Mulungu, iye ndi munthu monga inu muliri, wakhala pano usikuuno. Iye timakhulupirirabe Mulungu. Iye tikuyenera kukhulupirira kuti Mawu Ake ndi Choonadi. Ndipo Iye adzatsimikizira izo, kuti Icho ndi Choonadi, ngati titangokhulupirira izo.

⁶⁴ Tsopano tayang'anani pa chopinga chimene Abrahamu anali nacho. Chinthu choyambirira chinali zaka zake, usinkhu wa zaka sevente-faivi, ndipo Sarah kukhala wa sikisite-faivi. Iye anali atadutsa kusintha kwa moyo, kusintha kwa thupi. Mosakayikira koma chimene icho chinayima, zaka zambiri mmbuyomo. Iye anali atakhala naye monga mkazi wake. Anali mlongo wake wa theka, mwina anamutenga iye ali mtsikana wachichepere, ndipo anamukwatira iye. Ndipo iye analibe mwana. Iye anali wosabereka mwamtheradi. Ndipo tsopano ife tikupeza kuti, kuti achite izi, iye anachita kudzipatula yekha kwa anthu onse amene sanakhulupirire izo, kuti apangitse izo kukwaniritsidwa.

⁶⁵ Ine sindikutanthauza kuti mukuyenera kudzipatula nokha kwa anthu. Koma inu mukuyenera kudzipatula nokha ku miseche yonse ya kusakhulupirira, ndi kukhala kutali ndi izo. Pamene anthu akuti, “Ah, zinthu zimenezo sizimachitika! Limenelo ndi gulu la anthu amisala! Palibepo chinthu ngati chimenecho chikuchitika,” mungotseka makutu anu ndi kuchokapo. Musapereke chidwi chirichonse kwa izo.

⁶⁶ Baibulo linanena kuti “Abrahamu sanagwedezeke pa lonjezo la Mulungu, kudzera mu kusakhulupirira; koma anali wamphamvu, akupereka matamando kwa Mulungu.” Dzina lake linasinthidwa kuchoka kwa Abramumu kudzakhala Abrahamu, kusintha kwa dzina kunapangitsa dzina lake “atate wa mafuko.” Kodi inu mungalingalire mwamuna akukhala ndi mkazi wake, wokonedwa wake, amene iye anakhala naye tsopano kwa zaka zonsezi, ndipo tsopano penapake mu usinkhu wa zaka eyite, ndipo mkazi wake usinkhu wa zaka sevente, koma komabe opanda mwana mmodzi kapena chiyembekezo cha mwana, komabe ankadzinenera kuti iye anali “tate wa fuko.” Kodi mungalingalire kunyozedwa ndi mzake wodutsa amene akananena, “Tate wa mafuko, tsopano uli ndi ana angati pano?” Ndi kunyozedwa konse kumene iye anadutsamo!

⁶⁷ Koma Abrahamu sanadzandime paliponse nkomwe, pa kusakhulupirira. Iye ankakhulupirira kuti Mulungu ndi wokhoza kuchita zomwe Iye analonjezazo, kuti Mulungu

akanatsimikizira Mawu Ake, ziribe kanthu kuti zinatenga nthawi yayitali bwanji. Koma mmalo moti azifooka nthawi zonse, monga momwe timachitira, iye ankakhala wamphamvu nthawi zonse. “Ngati icho sichinachitike lero, mawa icho chidzakhala chozizwa chokulirapo, chifukwa icho ndi cha msinkhu wa tsiku limodzi.” Ameneyo anali Mulungu, ameneyo anali Mulungu mwa Abrahamu, pakuti iye ankadziwa kuti Mulungu anatsimikizira Mawu Ake onse kuti anali chomwecho.

Ngati ana Ake atangotenga Mawu Ake, kuti Iye athe kuwatsimikizira Iwo ndi inu! Imeneyo ndi njira yokhayo imene Iye angatsimikizire Mawu Ake.

Iye samawatsimikizira Iwo kwa osakhulupirira. Iwo sangatsimikiziridwe; iwo ndi osakhulupirira. Koma, Iwo si kwa osakhulupirira. Iwo si a osakhulupirira.

⁶⁸ Iwo ndi a kwa iye amene akhulupirira. Ndipo ngati Iye angakhoze kumupeza winawake amene angakhulupirire Mawu Ake, Iye adzatsimikizira Mawu Ake mwa inu. Ndipo nthawizina matenda ndi zinthu zimachitika kwa ife mwanjira imeneyo, kuti Mulungu akhoze kudzitsimikizira Yekha.

Kodi mukukumbukira munthu wakhungu amene Yesu anamupeza? Iwo anati, “Ndani anachimwa, iye kapena abambo ake, amayi ake?”

⁶⁹ Iye anati, “Mu nkhani iyi, palibe, koma kuti ntchito za Mulungu zidziwike.” Mwaona, zinachitikira kwa mnyamatayo kuti Yesu alemekzedwe. Nthawizina matenda si themberero, ndi mdalitso, kuti ife tikhoze kuyika chikhulupiriro chathu kunja uko ndi kuzitchula zinthu zimene kulibeko, ngati kuti izo ziripo. Mulungu ananena chomwecho, ndipo Iye adzatsimikizira kuti ziri chomwecho ngati inu simungafooke pansu pa mayesero.

⁷⁰ Iye akanamutsimikizira Yobu, nthawi ina, kuti iye sakanamutukwana Iye pamaso Pake. Taonani mayesero amene Yobu anakumana nawo. Koma pansu mu nsagwada za imfa, komabe iye anati, “Ambuye anapereka, Ambuye watenga, lidalitsike Dzina la Ambuye!” Iye ndithudi anazikhulupirira izo. Mulungu anatsimikizira Mawu Ake kwa Yobu. Iye anatsimikizira izo kwa Abrahamu. Iye anatsimikizira izo chomwecho.

⁷¹ Ndiponso Iye anatsimikizira izo mwa Mose. Ndipo pamene Mose, pamene vuto linamugwera iye, Mose anali nacho mmalingaliro ake, kuti mwina, kukhala wowombola, kuti mwina mayi ake anamuuzza iye kuti anabadwa ali mwana wabwinobwino. Iye—iye anali mphunzitsi wake amene anamulera iye mu nyumba yachifumu ya Farao, mosakayika anali atamuuzza iye, “Mwana, ife tapemphera kuti tiwomboledwe, ndipo ife tikukhulupirira kuti ndiwe mwana amene Mulungu ati amugwiritse ntchito kuti awombole.” Ndiyeno pamene iye. . .

⁷² Mwaona, iye anabwera ndipo anali woti adzakhale—mwana wa mwana wamkazi wa Farao, ndipo ife tikupeza kuti iye anali woti adzakhale wolowa ku mpandowachifumu. Bwanji, mosakaika izo zinali mmalingaliro awo pamenepo, kuti iye akanadzakhala Farao wotsatira, “Ndipo umo ndi momwe iye adzawombolere anthu, pokhala Farao wotsatira.” Koma Mulungu anali ndi. . . Ngati izo zikanakhala chomwecho, ndiye iye akanazichita izo kudzera mu zinthu, kudzera mu a—a—mchitidwe wa ndale. Koma Mulungu samagwira ntchito monga choncho nthawizonse.

⁷³ Mulungu ali nazo njira Zake zogwirira ntchito, ndipo Iye anati Iye “adzawatulutsa iwo.” Iye anamuza Abrahamu, “Zikadzatha zaka foro handiredwe,” Iye “akanadzawatulutsa iwo, ndi dzanja lamphamvu,” Iye “akanadzawonetsa zizindikiro ndi zodabwitsa.” Chotero iye sakanatha kuchita izo monga choncho, chotero Abra-. . . Iye tikupeza kuti Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndipo apa pali Mose tsopano akukhulupirira Mulungu.

⁷⁴ Ndipo Mose anayang’ana kunja kwa zenera lomwelo limene Farao analipanga, iye ankawayang’ana anthu omwewo. Amene Farao ankawayang’ana iwo, ngati, “Anthu otembereredwa, anthu omwe analibe kalikonse koma gulu la kutengeka, kwa Mulungu, ndipo Mulungu wina wa mchipululu kwinkwake amene iwo sankadziwa kalikonse ka izo; malo ena osawoneka amene iwo amapempherapo, kuti panalibe kanthu kwa izo. Iwo ndi gulu la otengeka. Ndipo iwo anali gulu la akapolo. Ndipo Mulungu wawo kulola iwo kukhala akapolo, anatsimikizira kuti Iye sanali Mulungu.”

⁷⁵ Ndipo pakati pa chinthu chonsecho, Iye ankazutsa munthu yemweyo. Mulungu amachita zinthu mwanjira yachirendo chotero, panso pa iwo omwe. Osati wazaumulungu, osati mphunzitsi, osati wansembe, osati mmodzi wa amuna awo oyera; koma munthu wamba chabe, wobadwira ntchitoyo. Ndipo Mulungu anamuyitana iye kuti adzakhale mneneri Wake, ndipo anamutumiza iye kumeneko. Ndipo opanda kanthu mu dzanja lake koma ndodo yopindika, kuti akakomane ndi gulu la nkondo, magulu okhala ndi zida amene anali atagonjetsa dziko lonse. Koma ali ndi ndodo imeneyo mdzanja lake, monga Mulungu anamuza iye kuti agwire ndodo imeneyo mdzanja lake ndipo iye akanadzawombola Israeli, ndipo iye anapita kumeneko ndipo anachita izo chifukwa Mulungu analonjeza izo. Kodi iye azichita motani izo? “Ine ndidzakhala ndi iwe.”

Iye anati, “Ndiwonetseni ine ulemelero Wanu, Ambuye. Ndine wochedwa kuyankhula. Ndimalaphera kuyankhula bwino. Ndipo ine. . .” Iye anali ndi zowiringula milioni.

⁷⁶ Koma Iye anati, “Ine ndidzakhala ndi iwe.” Ndipo ndizo zonse zomwe zinatengera. Iye anapita, akutenga Mawu a

Mulungu. Ziribe kanthu momwe ntchitoyo inkawonekera yowopsya, Mose anapitirira kumukhulupirira Mulungu. Ndipo Mulungu anatsimikizira Mawu Ake, kudzera mwa Mose, kuti anali choonadi. Chifukwa, mosalabadira chimene chinachitika, Mose anakhalabe ndi Mawu. Pa nthawi ya ulendo . . .

⁷⁷ Mulungu anawauza iwo, uko mu Igupto, aponso, kuti Iye akanadzawawombola iwo, “Kupita mu dziko lolonjezedwa, dziko labwino, lodzaza mkaka ndi uchi.” Ndipo ilo linali mwamtheradi kumeneko. Iwo sankadziwa kuti ilo linali kumeneko, koma Iye anati, “Ilo liri kumeneko, ndipo Ine ndakupatsa iwe ilo. Ilo ndi lako kale, ingopita ukalitenge ilo!”

⁷⁸ Ndipo mchipululu, pamene ambiri a iwo anatuluka, akuvina mu Mzimu, pamene Miriamu ankawomba nkhotcho; akudya manna ochokera Kumwamba; anamumvera Mose akuyimba mu Mzimu; akuwona zozizwitsa ndi zizindikiro zikupita. Koma pamene zinafika pa chiwonetsero, kuti akhulupirire Mawu onse a Mulungu, malonjezo onse, iwo analephera.

Awiri okha a iwo anakhulupirira izo, amenewo anali Yoswa ndi Kalebu. Ndipo iwo anabweretsa umboni wosonyeza kuti dzikolo linali labwino.

⁷⁹ Koma, zochitikazo zinali, ndi zimene zinawalepheretsa iwo. Chifukwa, iwo anati, “Ife sitingathe kulitenga dzikolo, chifukwa mizinda yawo ili ndi mipanda, zawo—zawo—nthumwi zawo kumeneko. Osati nthumwi zawo, koma awo—anthu awo ndi zimphona zazikulu. Bwanji, ife tikuwoneka ngati zitete, pambali pa iwo.”

⁸⁰ Yoswa ndi Kalebu anati, “Ndife okhoza kulitenga ilo.” Chifukwa chiyani? Mulungu anali atalipereka ilo kwa iwo, ziribe kanthu momwe zimphonazo zinali zazikulu. Chopingacho sichinali kanthu kwa iwo. Mulungu anali atanena chomwecho! Ndipo Mulungu anatsimikizira izo ndi iwo. Ndipo iwo anapita ndipo anakalitenga dzikolo, monga Mulungu ananenera kuti iwo akanadzachita izo. Iye anatsimikizira izo kwa iwo.

⁸¹ Tsopano, pamene iwo anadzabwera mu mwezi wa Epulo, pamene madzi anali kuwulukira pansi kuchokera mmapiri, pamwamba pa mathithi a chipale chofewa, ndi zina zotero, ndipo zimawoneka ngati kuti Mulungu anali wamkulu wankhondo wosauka, kuti awatsogolere ankhondo Ake mpaka ku maloko, Iye anawakanikiza iwo kuchoka ku dziko lolonjezedwa. Ndipo nthawi yomweyo imene Iye anawatenga iwo, anali woti awatenge iwo, iwo unali mwezi woyipitsitsa mu chaka. Mwezi umene Yordano ankasefukira magombe ake, anathamangira ku minda. Bwanji, ngati iwo akanati awalande iwo, iyo ikanakhala mu nthawi ya chirimwe, pamene iwo akanatha kuwoloka. Koma Iye anadikirira mpaka madzi azame. Iye amakonda kuwonetsera kuti Iye ndi Mulungu. Iye amakonda kutsimikizira Mawu Ake, mosalabadira.

⁸² Osadandaula ngati adokotala anati, “Mufa ndi khansa.” Ndizo zonse zimene munthu amadziwa. Mwinamwake madzi ndi akuya kwa ena a inu, usikuuno. Koma, kumbukirani, Mulungu anapanga lonjezo. Mulungu amasunga Mawu Ake, ndipo Mulungu amatsimikizira Mawu Ake. Icho ndi Choonadi.

⁸³ Iye anadikirira mpaka madziwo atachita matope, mpaka iwo atafika pakuya ndipo pamwamba pa mitu yawo, ndi zina zotero, ndipo kenako Iye anadzatssegula njirayo. Iye anapita patsogolo pawo ndipo anapanga njira.

⁸⁴ Iwo alowa bwanji mkati, ku Yeriko, pamene iyo yonse inali itatsekedwa? Yoswa ankadabwa. Iye ankadziwa kuti Mulungu anali atamutsogolera iye kutali chotero, sitepe yotsatira ndi ya Mulungu.

⁸⁵ Tsiku lina, pamene iye anali kunja akuyenda mozungulira, akuyang’ana makoma, iye anawona Mwamuna atayima ndi lupanga Lake atalisolola. Ndipo iye anasolola lupanga lake ndipo anapita kukakumana ndi Munthuyo, iye anati, “Iwe ndi wa Ndani? Kodi Iwe uli ndi ife kapena Iwe ndi mdani wathu?”

⁸⁶ Iye anati, “Ine ndi Kapitawo wa khamu la Ambuye.” Ndipo Iye anamuza iye choti achite. Kodi iye aliza bwanji lipenga ndipo khoma nkugwa pansu, lakuti iwo amathamangitsapo mjaha wa magaleta kudutsa pa iwo? Zingakhale ndi chochita chanji ndi lipenga?

⁸⁷ Mulungu amagwiritsa ntchito njira zophweka chomwecho. Ndi choncho, kuphweka kwake, chimene chimapanga Mulungu kwa ine. Nthawizonse timayetsa kuti tipeze chinachake chachikulu, chichita chinachake, ndi Mulungu. . . bungwe lina lalikulu litenga chinthu chonsecho ndi kuchichotsa chonsecho. Pamene, Mulungu amatenga munthu wophweka, munthu mmodzi yekha amene Iye angamugwire mmanja Mwake, ndipo Iye adzatsimikizira Mawu aliwonse amene Iye ananena, ndi Iwo. Zimatengera njira zazing’ono zophweka ngati izi!

⁸⁸ “Ombani lipenga.” Osati kumbani khomalo, koma, “Mungowomba lipenga, ndipo makomawo agwa. Kuwomba kwa lipenga kudzagwetsera pansu makomawo.” Ndi zopusa bwanji kwa malingaliro achithupi! Koma Mulungu anatsimikizira Mawu Ake kuti anali owona, pakuti makomawo anagwera pansu, limodzi pamwamba pa limzake. Iwo anapita molunjika ndipo anakatenga mzindawo.

⁸⁹ Oh, Mulungu amakonda kudzitsimikizira Yekha kuti ndi Mulungu! Yoswa ankadziwa zimenezo. Tsiku lina, ndipo pamene iye anayima pamenepo, chimodzi cha zododometsa zazikulu zimene zinayamba zachitikapo, kunja kwa imfa, kuikidwa mmanda, ndi kuwuka kwa Yesu Khristu. Pamene mdani . . . Iye anali atawagonjetsa iwo, ndipo ankhondo osiyanasiyana anali mmapiri. Iye anawagonjetsa iwo, ndipo dzuwa linkalowa. Oh, mai, inali nthawi yotani kwa Mtsogoleri Yoswa!

⁹⁰ Kumbukirani, iye anamenyana ndi dziko limenelo, wopanda chipatala, namwino, gulu la chithandizo choyamba, kapena anali ndi munthu wovulala. Ndiuzeni chinachake chimene chingagonjetse zimenezo. Inde, bwana. Iye analibe konse zipatala, opanda anamwino, ndipo iye sanatayepo munthu aliyense, bola ngati iwo ankayenda mu chifuniro ndi Mawu a Ambuye. Mulungu anatsimikizira kuti Iye anali ndi iwo. Uko nkulondola. Zindikirani tsopano.

⁹¹ Ndipo ife tikupeza kuti Yoswa anadziwa, ngati usiku ubwera, iwo akanadzazemba ndi kukomana wina ndi mzake, ndi—ndi kudzisonkhanitsa okha pamodzi ndi kupanga gulu lina lalikululu lankhondo, ndipo iye akanakhala ndi nthawi yovuta ndi iwo tsiku lotsatira. Iye sankadziwa choti achite, chotero iye anayang’ana mmwamba kwa Mulungu. Iye ankafunikira thandizo, ndipo iye ankafunikira dzuwa limenelo kuti liime. Chotero iye anangolamula kuti dzuwa liyime nji, ndipo a . . . anati kwa “mwezi ukhale pamwamba pa Ajaloni,” usasunthe mpaka iye atalamula izo. Ndipo mwezi ndi dzuwa zinayima kwa maora twente-foro, pamene Yoswa ankamenya nkhondo ndipo anamgonjetsa mndaniyo, chifukwa iye anali kumene mu mzere wa ntchito. Iye anali ndi ufulu wochita izo, chifukwa iye ankamvera lamulo la Mulungu.

⁹² Ndipo bola ngati iwe uli mu mzere wa ntchito, ukusunga Mawu a Mulungu, ukuchita basi chimene Iye anakuuza iwe kuti uzichita, kumaguba mwa kulamula kwa Mulungu, umakhala ndi ufulu wonena kwa phiri ilo, “Suntha!”

⁹³ Mulungu amasunga Mawu Ake. “Mukanena kwa phiri ili, ‘Suntha,’ osakayikira mumtima mwanu, koma kukhulupirira kuti chimene mwanena chichitika, inu mukhoza kukhala ndi chimene mwanenacho.” Yesu ananena izo, mu Marko Woyera 11:22. Ndicho Choonadi. Ine ndikudziwa icho ndi Choonadi. Ndi Mawu a Mulungu, ndipo izo zikutsimikizira kuti ndi Choonadi. Ife timangochita mantha nthawizina. Ife tikafika pa malo, timawopa kuti Iye sakwaniritsa Mawu amenewo. Iye adzakwaniritsa Mawu amenewo. Iye anati Iye akanadzachita izo. Tsopano, ife tikupeza kuti izo nzoona. Iye anatsimikizira izo.

⁹⁴ Uneneri wa Yesaya, nthawi ina, chinthu chimene chinali chisanachitikepo; chinali chisanachitikepo nkale lonse, ndipo sichinachitikepo chiyambireni. Iye anati, “Namwali adzayima.” Kodi inu mungalingalire mkazi, popanda kumudziwa mwamuna, akanadzakhala ndi mwana? Yesaya anati, “Namwali adzayima.”

Ndipo Mulungu anapangitsa namwali kuti ayime, kuti atsimikizire Mawu Ake kukhala choonadi. Iye anatsimikizira Mawu Ake, chifukwa namwali anaima ndipo anabala Mwana wamwamuna.

⁹⁵ Tsopano, Mawu aja atasandulika thupi, penyani chimene Iwo anachita. Pamene Mwana ameneyo anabwera, Iye anali Mawu Iyemwini. “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.”

⁹⁶ Iye anali Mawu amoyo amenewo. Iye anatsimikizira kuti Iye anali Mawu amoyo amenewo. Iye anati kwa aphunzitsi a tsiku limenelo, “Ndani anganditsutse Ine za tchimo?” *Tchimo* ndi “kusakhulupirira.” “Ndani angandiuze Ine kuti ndine wosakhulupirira? Mawu aliwonse amene analembedwa a Ine, akwaniritsidwa.” Maulosi seveni otsiriza a moyo Wake anakwaniritsidwa mu maora seveni otsiriza, pa mtanda. Chirichonse chinalembedwa za Iye, chinakwaniritsidwa, chifukwa Iye anali Mawu. Iye anatsimikizira kuti Iye anali, anali. Iye anachiritsa odwala. Iye anaukitsa akufa. Iye anagonjetsa imfa, hade, ndi manda. Iye anatsimikizira kuti Iye anali Mawu.

Zindikirani nkhani iyi kunyumba ya Yairo. Iye anali. . . Iye anali atawauza iwo choonadi. Ife tikumuona Iye pamene Iye anawoloka nyanja. Iye akulowa.

⁹⁷ Panali mkazi wamng’ono pamwamba pa phiri, amene anali atawononga ndalama zake zonse kwa asing’anga. Mosakaika, asing’anga anali atachita zonse zimene iwo ankadziwa momwe angachitire, kuti amuchiritse mkaziyo; mwinamwake asing’anga Achihebri, ndipo ameneyo anali mkazi Wachihebri, chotero iwo anali atamchitira zonse zimene iwo akanatha mlongo wawo. Ngakhale, iwo analibe kanthu koletsa vuto la magazi limeneli, limene linali, mwinamwake, nthawi ya kusintha kwa thupi ndipo magazi ake anali atayenderera mpaka iye. . . kanthu kakang’onoko kanali katafooka kwambiri moti sankathanso kuyenda. Ndipo iye anali atamva za Yesu. Ndipo pamene iye anawona bwato laling’ono likukankhira mu misonododzi, iye anapita kumusi kuti akafufuze.

⁹⁸ Ambiri a otsutsa Ake anali atayima pamenepo. Ndipo Iye sali opanda otsutsa lero. Ngati iwo akanadziwa Yemwe Iye anali, iwo sakanakhala otsutsa Ake. Koma iwo anali otsutsa Ake chifukwa iwo sankadziwa Yemwe Iye anali.

Ndipo umo ndi momwe ziriri ndi Uthenga lero, amuna ndi akazi ambiri abwino amatsutsa Iwo chifukwa samadziwa chimene Iwo ali.

⁹⁹ Yesu anati, “Ngati inu mukanamudziwa Mose, inu mukanandidziwa Ine. Mose ankayankhula za Ine. Amuna aakulu ambiri amalalakala atawona tsikuli. Ngati Ine sindichita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine. Ine ndiri ndi umboni wochulukuka,” Iye anati, “kuposa uja wa Yohane, pakuti ntchito zimene Ine ndikuzichita, zikutsimikizira kuti Atate ali ndi Ine.” Iye anali ndi ntchito zazikulu, chifukwa Iye

anali Wozindikiritsidwayo. Yohane anazindikiritsidwanso, monga liwu la wofuula mchipunulu. Koma pamene Iye anabwera, Iye anali mneneri amene Mose anamuyankhula kuti adzaukitsidwa.

Monga ine ndinanenera usiku wina, Iye anabwera mu maina atatu; dzina la Mwana wa Mulungu, Mwana wa munthu, ndi Mwana wa Davide.

¹⁰⁰ Pamene Iye anali pa dziko lapansi pano, nthawi yoyamba, Iye anali Mwana wa munthu. Iye sakanakhala Mwana wa Mulungu nthawi imeneyo; Iye sankadzinenera konse kuti anali. Iye anati Iye anali “Mwana wa munthu.” Pamene aliyense akanamufunsa Iye, Iye anati, “Inu mukuwona Mwana wa munthu; Mwana wa munthu.” Tsopano, “Mwana wa munthu” ndi *mneneri*. Iye ankayenera kubwera mwanjira imeneyo, chifukwa, Lemba, Iye sangabwere motsutsana ndi Lemba.

¹⁰¹ Ndi chifukwa, lero, kuti wathu—Uthenga wathu wa ora lino sungathe kubwera kupyolera mwa azaumulungu ndi zaumulungu, iwo ukuyenera kubwerera ku chinthu chomwecho chimene iwo unalonjeza kuti udzachita. Izo zikuyenera kukhala mwanjira imeneyo.

¹⁰² Chotero ife tikupeza kuti, mwa Munthu uyu, Iye ankayenera kudzakhala mneneri. Osati Mwana wa Mulungu pamenepo, Iye ankayenera kudzakhala Mwana wa munthu. Yehova Iyemwini ankawatcha aneneri, Yeremiya ndi iwo, “Mwana wa munthu.” “Mukadzawona Mwana wa munthu...” “Mwana wa munthu ndi ndani?” iwo anakhala akufunsa.

¹⁰³ Kenako, Iye anatumikira udindo Wake ngati Mwana wa munthu. Kenako Iye anatumikira udindo Wake tsopano ngati Mwana wa Mulungu. Mulungu ndi Mzimu, ndipo pamene tsopano Iye ankatumikira kudutsa mu Mibadwo ya Mpingo, monga Mwana wa Mulungu. Tsopano, mu Zakachikwi, Iye adzakhala Mwana wa Davide, pamene Iye adzakhale pa mpando wachifumu wa Davide. Iye adzakhala wolowa ku mpando wachifumu, Mwana wa Davide. Mwana wa munthu, Mwana wa Mulungu, Mwana wa Davide, ndipo ndi Munthu yemweyo nthawi zonse.

¹⁰⁴ Monga ngati Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera; udindo wa Mulungu. Iye anali Mulungu Atate, kenako Iye anadzakhala Mulungu Mwana, tsopano Iye ndi Mulungu Mzimu Woyera. Osati a Mulungu atatu; Mulungu mmodzi, mawonetseredwe atatu, zikhumbo zitatu za Mulungu yemweyo.

Tsopano ife tikupeza, ndipo mu ora lino limene ife tikukhalamo tsopano, Mulungu akusunga Mawu Ake mofanana basi monga Iye ankachitira nthawi imeneyo.

¹⁰⁵ Ife tikupeza kuti Iye anabwera anadzawoloka nyanja. Mkazi uyu anamukhulupirira Iye, panali chinachake mkati mwake chinayamba kugunda. Iye analibe Lemba la izo, analibe Lemba

chimodzimidzi monga Yoswa anachitira kuti aliyimitse dzuwa, koma iye anakhulupirira mu mtima wake kuti Iye anali Mwana wa Mulungu. Chotero iye anati, “Ngati ine ndingakhudze kokha chovala Chake, ine ndichiritsidwa.” Chotero iye anakankha kudutsa mu khamulo mpaka anakakhudza chovala Chake, ndipo vuto la magari linatha.

¹⁰⁶ Tsopano, Iye anayang’ana pa omvetsera, kuti apeze amene anamukhudza Iye. Mosakayikira, panali winawake. Iye anayima. Anthu onse anamuunjikira Iye; ndipo ena akumusereula Iye, ena akumuseka Iye; wansembe atayima pambali ndi kumufunsa Iye, ndi azibusa, ndi ena otero. Koma panali ena amene anamukhulupirira Iye. Ndipo, ndipo patapita kanthawi Iye anaima, mwadzidzidzi, anatembenuka, anati, “Ndani wandikhudza Ine?”

¹⁰⁷ Ena a iwo anati, “Bwanji, Ambuye!” Ine ndikukhulupirira anali Petro anati, “Bwanji, khamu lonse lakuunjikirani Inu. Bwanji, ndani ‘wakukhudzani’ Inu? Bwanji, aliyense akukukhudzani Inu!”

Iye anati, “Koma Ine ndazindikira kuti mphamvu zachoka kwa Ine.” Iye anafooka. Kunali kukhudza kosiyana.

¹⁰⁸ Ngati ife tingakhoze kokha kuwona izo, m’bale, mlongo! Ngati inu mungamukhudze Iye ndi kukhudza kwina kumeneko! Oh, anthu odwala, ine ndikukonzekera kuti ndikupemphererani inu, mu maminiti ochepa chabe. Ine ndikukhulupirira kuti ndiri nawo Mzimu Woyera, sikuti ndi Mzimu Woyera kuposa umene inu muli nawo kunjira uko, amuna awa ali nawo pano. Mzimu Woyera womwewo, koma ndi lamulo la Mulungu; ndipo ngati inu muti mukhulupirire kuti ilo ndi lamulo la Mulungu, la kupempherera odwala, ndi kusanjika manja pa iwo, ndi kutulutsa mizimu yoyipa, ndi malonjezo amene Iye wapanga, chikhala chinthu chomwecho ndi inu. Mupeza chimene mukuchipempha, ngati mungathe kukhulupirira izo.

“Kodi ungakhulupirire kuti Ine ndikhoza kuchita izi?” anatero Yesu.

¹⁰⁹ “Eya, Ambuye, ine ndikukhulupirira,” anatero bambo wamwana wakhunyuyo, “Ine ndikukhulupirira kuti Inu ndi Mwana wa Mulungu amene anali woti adzabwere mdziko.” Tsopano, ife tikudziwa kuti izo zikhoza kungotengera khalidwe limenelo kuti zibweretse zotsatira.

¹¹⁰ Tsopano, mwachangu, tiyeni tiganizire za Iye kamphindi, apa Iye ali pa njira Yake yokwera. Wansembe wamng’ono anabwera, mosakayika koma munthu wamng’ono ameneyo anali wokhulupirira wammalire.

¹¹¹ Alipo ochuluka a iwo mdziko lero, okhulupirira aang’ono ammalire. Iwo amafuna kukhulupirira Izo. Iwo amafuna kuti akhulupirire kuti Mzimu Woyera ndi weniweni. Iwo amafuna kukhulupirira kuti uku ndi kusuntha kwa

utumwi, monga momwe Mulungu analonjezera mmasiku otsiriza Iye adzatsanulira Mzimu Wake. Ife... iye akufuna kukhulupirira mu Malaki 4, kuti Iye analonjeza, mu masiku otsiriza—Chikhulupiriro chapachiyambi cha chipentekoste chikanadzabwezeretsedwanso kwa—kwa mpingo kenanso.

¹¹² Malaki 4 amanena zimenezo. “Taonani, Ine ndidzakutumizirani inu Eliya mu tsiku lotsiriza,” uko nkulondola, “ndipo iye adzabwezeretsa Chikhulupiriro cha ana kubwerera kwa atate kenanso,” mwaona, “Chikhulupiriro cha atate kwa ana, aponso.” Mwaona, izo zikuyenera kukhala.

Inu mukuti, “Chabwino, ameneyo anali Yohane M’batizi.” Ayi, ayi.

¹¹³ Yohane M’batizi anali Malaki 3. Uko nkulondola. Mateyu 11 amanena chomwecho, “Ngati mungalandire icho, uyu ndi iye amene akunenedwa, “Taonani, Ine ndatuma mthenga Wanga patsogolo pa nkhope Yanga.” Uyo anali Eliya, ndithudi. Yesu anati anali. Koma osati Eliya wa Malaki 4, nkomwe.

¹¹⁴ Chifukwa, “Mwamsanga pambuyo pa Uthenga umenewo, dziko lapansi lidzathedwa ndi moto, ndipo olungama adzayenda pa phulusa la oyipa.” Chotero izo sizinachitike mu nthawi ya Yohane. Ife tikuyenera kukhala ndi Uthenga ukusesa mmbuyo ndi kuwabweretsa anthu mu zikholidwe zonse izi zachipembedzo, kubwerera ku chapachiyambi, Chikhulupiriro chenicheni cha chipentekoste. Ndipo ife tikuziwona izo zikuchitidwa, ndiko kukwaniritsa kwa Lemba limene likuyenera kukwaniritsidwa. Malemba onse akuyenera kukwaniritsidwa. Ndi zochulukira bwanji za izo zimene ife tingathe kuziika, zinganditengere ine motalika kuposa nthawi yanga pano, kuti ndiwonetsere. Koma inu mukumvetsa zinthu izi, kuti zikuyenera kuchitika ndendende monga chonchi, kwa ana a Abrahamu, monga Iye analonjezera.

¹¹⁵ Tikumuwona Yesu akupita tsopano kukamchiritsa mtsikana wamng’ono. Chifukwa, atate, wokhulupirira wamng’ono wa mmalire, chinachake chinafika pa malo akuti iye ankayenera kumuzindikira Yesu, chotero, adokotala anali atamusiya iye. Ndipo iye anavala chipewa chake chaching’ono chakuda ndipo ananyamuka kuti akafufuze ngati iye akanatha kumupeza Yesu. Mwaona, Iye nthawizonse amakhala pamenepo pamene inu mukumufuna Iye. Iye anamupeza Iye akubwera m’mphepete mwa nyanja.

¹¹⁶ Ndipo iye anati, “Bwerani kwa mtsikana wanga wamng’ono, mudzayike manja Anu pa iye, ndipo iye akhala bwino.” Anati, “Iye wagona watsala pang’ono kufa. Iye ndi mwana wanga yekhayo.” Anati, “Iye ndi wausinkhu wa zaka thwelofu. Ife tiribe ana ena. Mkazi ndi ine,” mwina, “tikukalamba. Ndipo uyu ndi mwana yekhayo amene tiri naye, ndipo iye wagona watsala

pang’ono kufa. Ambuye, ine ndikukukhulupirirani Inu. Ngati Inu mungabwere kudzaika manja Anu pa iye, iye akhala bwino.”

Mwaona, kodi iye anazindikira chiyani? Iye anazindikira kuti Mawu olonjzedwa a Mulungu aja anawonetseredwa mwa Munthu uyu.

¹¹⁷ Chimodzimodzi basi monga momwe Nikodemo ananenera, “Rabbi, mphunzitsi, ife tikudziwa kuti Inu ndi mphunzitsi wochokera kwa Mulungu. Ife tikuzidziwa izo. Afarisi akudziwa zimenezo.” Nchifukwa chiyani iwo sanavomereze izo? “Palibe munthu angathe kuchita zinthu zimene Inu mukuchitazi, pokhapokha ngati Mulungu atakhala ndi Iye. Ife tikudziwa kuti Inu munachokera kwa Mulungu.”

¹¹⁸ Apa ife tikupeza kuti Yairo anakhulupirira chinthu chomwecho. Iye anati, “Bwerani mudzayike dzanja Lanu.” Iye anadziwa kuti Mulungu anali mwa Iye. “Dzaikeni manja Anu pa mwana wanga. Ngakhale ali pafupi kufa, iye akhala moyo.”

¹¹⁹ Iye anangoyenda limodzi ndi iye. Ndipo pamene iye ankapita, apa panadzabwera wothamanga akubwerera, ndipo anati, “Usamuvutitse Iye, usamuvutitsenso Ambuye. M—mtsikanayo, wafa, iye wapita tsopano. Iye wapita.”

Yesu anatembenukira kwa Yairo, anati, “Kodi Ine sindinati kwa iwe, ‘Ngati iwe ungakhulupirire, uwona ulemelero wa Mulungu?’ Ngati iwe ungakhulupirire izo!”

¹²⁰ Iye analowa mchipinda, ndipo apo iwo anali, onse akulira ndi kulira, ndi kubuula, chimodzimodzi monga momwe anthu aliwonse angachitire. Mtsikana wamng’ono wabwino, mwana wamkazi wa abusa, anali atamwalira, ndipo iye anachotsedwa mdziko lino. Ndipo mwinamwake anali atafa kwa maora, ndipo kenako iwo anali atamugoneka iye pa mpando, ndipo anali wokonzeka kuti akonze thupi lake, mwinamwake, ndi kukamuyika iye, ndi kuikidwa mmanda.

Kenako tikupeza kuti Yesu analowa mnyumbamo. Onse anali akulira. Iye akuti, “Perekani mtendere.” Iye anati, “Iye sanafe, koma iye akugona.”

¹²¹ Tsopano kodi mungalingalire zimene iwo anaganiza? “Bwanji, munthu uyu ife tikumudziwa, tsopano. Ife tikudziwa kuti Iye ndi mwana wapathengo. Ndipo ife tamva za Ake, maulosi Ake onse aphuma amene Iye amawapanga. Ndipo tsopano ife tikudziwa kuti wansembe akulondola, ‘mwamunayo wapenga,’ chifukwa tikudziwa kuti iye wafa. Adokotala anena kuti iye ‘wafa,’ ndipo apo iye wagona. Iye wapita, ndipo ife tikudziwa kuti wafa.” Iwo anati, iwo anamuseka Iye monyoza, mwa kunena kwina, anamupangitsa Iye kuchita manyazi, pomutsutsa Iye.

¹²² Koma Iye anali atanena kale kuti iye sanafe. Ndizo zonse zimene zimafunikira. “Iye wagona.” Ziribe kanthu otsutsa achuluka bwanji, Iye atsimikizira Mawu Ake! Iye anawatulutsa onse mnyumbamo, anawachotsa osakhulupirira onse. Anamutenga Petro, Yakobo, ndi Yohane, okhulupirira, mboni zitatu, ndi abambo ndi amake, anadzalowa ndipo anamugwira mwana wamkaziyo pa dzanja, ndipo anayankhula mu chinenero chimene chinaitanira moyo wake kubwerera kuchokera kwinakwake kutali mu Muyaya. Ndipo mtsikanayo anadzakhala moyo.

¹²³ Kodi Iye anachita chiyani? Iye anatsimikizira Mawu Ake. Iye anatsimikizira icho chimene Iye ananena. Iye sanali wakufa. Iye anali mtulo. Tsopano ife tikupeza, pochita izi, pozindikira, ndipo Iye anatsimikizira chinachakenso pamenepo. Tsopano Iye anatsimikizira kuti Iye anali Mulungu. Iye anatsimikizira kuti Iye anali ndi kudziwiratu. Penyani chimene Mawu Ake ananena tsopano. “Iye sanafe, koma iye wagona.” Mwaona, iye sanali atafa, kuyamba ndi kuyamba. Iye anali atagona. Anawonetsera kudziwiratu Kwake. Tsopano, pakhoza kukhala kuti panali anamwali ambiri omwe anafa mmawa womwewo, koma uyu anali asanafe. Iye anali akugona, monga momwe zinamuchitikira Lazaro. Ndipo Iye anamuyitana iye kuchokera mu tulo limenelo, chifukwa iye anali asanafe.

¹²⁴ “Ndipo iye amene akhulupirira mwa Ine, ngakhale iye atafa, komabe iye adzakhala ndi moyo; ndipo aliyense amene ali moyo ndipo nakhulupirira mwa Ine, sadzafa konse.” Iwo okha amene ali pa Bukhu la Moyo la Mwanawankhosa, amene Iye anawawombola pamene Iye anafa, iwo ndi amene Iye adzawaitana kuchokera mu tulo limenelo, pa tsiku limenelo, iwo amene afulumizitsidwa ndi mphamvu Yake, amene ali ndi mphamvu yofulumizitsa iyo ili mwa iwo. Ngakhale monga ine ndinanena usiku watha; ngakhale Elisha atafa, ndipo mafupa ake anali mmanda, mphamvu yofulumizitsa imeneyo inali ikadali pa mafupa ake.

¹²⁵ Zedidi, Iye anatsimikizira Chimene Iye anali. Tsopano ife tikupeza kenanso, chimodzimidzi, Iye anatsimikiziranso, kuti, mu Ahebri mutu wa 4 ndi ndime ya 12, Iye anatsimikizira kuti Iye anali Mawu a Mulungu. Iye ndithudi anatero. Zindikirani chimene Iye anachita. Ahebri, 12, Ahebri 4:12 amanena kuti, “Mawu a Mulungu ndi amphamvu kwambiri, achangu kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ndipo—ndipo Iwo ndi Ozindikira malingaliro ndi zokhumba za mu mtima.” Penyani mphindi yokha tsopano.

¹²⁶ Pamene Iye anayamba koyamba utumiki Wake, Iye atatuluka kudzawonetsera kuti Iye anali Mawu, pamene Iye anabwera kuchokera ku chipululu kuchokera ku yesero Lake, panali mwamuna wotchedwa Petro, dzina lake ndiye linali Simoni. Ndipo iye anabwera kwa Yesu ndi mchimwene wake, Andreyana.

Ndipo mwamsanga pamene iye anayenda mu Kukhalapo kwa Yesu Khristu, Yesu anati, “Dzina lako ndi Simoni. Ndipo la abambo ako linali Yonasi. Kuyambira pano udzitchedwa Petro.” Izo zinatsimikizira kuti Iye anali Mawu, chifukwa Mawu ndi Ozindikira maganizo ndi zokhumba zamu mtima. Iye anali Mawu.

¹²⁷ Filipino anaziwona izi zikuchitika. Iye ananyamuka akuzungulira phiri, anali atapita kwa tsiku, ndipo anabwerera. Ndipo iye anabwera limodzi naye mzake wotchedwa Natanieli. Ndipo iye anati, “Zinthu izi zikuchitikadi. Mose anati ‘Ambuye Mulungu wathu adzautsa Mneneri’ wonga iye, ndipo Munthuyo ndi ameneyu. Bwanji, Iye wamuuza Simoni yemwe iye anali, ngakhale yemwe abambo ake anali, ndipo ife tikudziwa kuti zimene Iye ananena ndi choonadi. Chifukwa, Mulungu ananena izo mu Mawu, ndipo apa izo zatsimikiziridwa kuti Iye anali woti adzachite izo, ndipo izo zikutsimikizira kuti ameneyo ndi Mesiya.”

Ndipo pamene iye anayenda mu Kukhalapo Kwake, Yesu ananena kwa iye, anati, “Taonani m’Israeli, amene mwa iye mulibemo chinyengo.”

Iye anati, “Rabbi, Inu munandidziwa liti ine?”

Anati, “Filipo asanakuitane iwe, pamene iwe unali pansu pa mtengo, Ine ndinakuwona iwe.” Iye anatsimikizira Mawu Ake. Iye anatsimikizira Mawu a Mulungu. Iye anatero.

¹²⁸ Mkazi pa chitsime, pamene iye anali... Chabwino, Iye anamupempha iye kuti Iye amwere madzi a mu mtsuko umene ankatungira madzi kuchokera pa chitsime, ndipo iye anati, “Si mwambo wake kuti inu Ayuda mutipemphe ife akazi Achisamariya chinthu chotero monga icho, chifukwa ife tiribe chochita.”

Iye anati, “Koma ukanadziwa Amene iwe ukuyankhula naye, ukanandipempha Ine akumwa.”

Iye anati, “Chitsimechi ndi chakuya.”

Ndipo kukambiranako, pamene kunali kupitirira, potsiriza Iye anapeza chimene vuto lake linali. Ndipo Iye anati, “Pita ukamutenge mwamuna wako, ndipo ubwere kuno.”

Iye anati, “Ine ndiribe mwamuna aliyense.”

Iye anati, “Iwe wanena zoono, wakhala nawo faivi, ndipo amene uli naye tsopano si mwamuna wako.”

¹²⁹ “Bwanji,” iye anati, “bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndi mneneri.” Iye... “Ife sitinakhale naye mmodzi kwa zaka foro handirede, inu mukudziwa.” Anati, “Ine ndazindikira kuti Inu ndi mneneri. Tsopano, ife tikudziwa kuti pamene Mesiya adzabwera, wotchedwa Khristu, pamene Iye adzabwera, Iye adzatiuza ife zinthu za mtundu uwu. Icho chidzakhala chizindikiro Chake.”

Pamene Iye anati, “Ine ndine Iye amene ndimayankhula ndi iwe,” Iye anatsimikizira Mawu Ake. Iye . . . ife tikutsimikizira chimene Iye ankadzinenera kuti ali. Iye anali Mesiya, Mwana wa Mulungu.

¹³⁰ Tsopano ife tikupeza, aponso, kuti mkazi wamng’ono uyu amene anali ndi vuto la magazi, amene anakhudza chovala Chake, izo zinatsimikiziranso kwa iye kuti Iye anali Mawu a Mulungu.

¹³¹ Tsopano kumbukirani, usikuuno, Yesu anati . . . Ndiponso, mu Ahebri, 1, Ahebri mutu wa 3, ine ndikukhulupirira ndi umenewo, Iye anati, “Iye tsopano ndi Wansembe Wamkulu,” m’badwo uno umene ife tikukhalamo tsopano, “Wansembe Wamkulu atakhala mu Ukulu wa Mulungu, Mmiyamba, amene angakhudzidwe ndi kumverera kwa zofooka zathu.”

Ahebri 13:8 amati, “Iye ali yemweyo, dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Iye ndi Mulungu yemweyo amene Iye anali nthawi imeneyo. Ali yemweyo usikuuno.

¹³² Yohane Woyera 14:12, Iye anati, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita. Ngakhale zochuluka kuposa izi iye adzazichita, pakuti Ine ndikupita kwa Atate Anga.” Mukuona? “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito izi zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita.”

¹³³ Mu Mateyu 28, Iye anati, “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silidzandiwonanso Ine, komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu kufikira chimaliziro cha dziko lapansi.”

¹³⁴ Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye akuyima, usikuuno, kuti atsimikizire Mawu Ake. (Nthawi yanga yatha.) Koma Iye anatsimikizira kuti Iye akanatero. Iye anatsimikizira Mawu Ake pamenepo, chimene Iye analonjeza kwa tsiku limenelo. Iye anatsimikizira mawu a Yesaya. Iye anatsimikizira mawu a Nowa. Iye anatsimikizira mawu a Mose. Iye anatsimikizira mawu aliwonse a aneneri.

¹³⁵ Iye analonjeza kuti mu tsiku lino, tsiku limene ife tikukhalamoli, kuti dziko likanadzakhala mu chikhalidwe cha Sodomu, amuna ogonana okhaokha. Tangoyang’anani pa izo mu dziko lero, konsekonse padziko kumene ine ndimapita; osati kuno kokha, kulikonseko. Ndi zosautsa. Mu Sweden, anyamata ndi atsikana amapita kumakasewera, ali maliseche. Ndipo iwo mu Germany ndi ku France, ndi kwina kulikonseko, ndi pafupifupi mtundu wabodza umene ife tiri nawo kuno ku United States. Ndi m’badwo. Ine, ngati ndingapeze mwayi wobwereranso, ndikufuna kuti ndidzayankhule pa zina za zinthu za uneneri, kwa inu, kuti ndidzakuwonetseni inu zimenezo, m’badwo umene ife tikukhalamowu. Baibulo linanena kuti, “Ana adzalamulira makolo awo.” [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi].

136 . . . Mawu. Koma, kumbukirani, Abrahamu anali ndi mbewu, imene inali mbewu Isaki. Iye anali ndi mbewu zina pambuyo pa imfa ya Sarah. Ndipo iye anali wa usinkhu wa zaka handirede ndi forte-faivi, iye anakwatira mkazi wina, anali ndi ana aamuna seveni pambali pa ana aakazi, chifukwa Mulungu anali atamutembenuza iye kukhala mnyamata pamene iye anali wa usinkhu wa zaka handirede. Iye anali kenanso forte-faivi, chotero ndiye iye. . . Ife tikudziwa zimenezo. Ine ndinalalikira izo kwa inu kuno mu California, zaka zapitazo.

137 Ndipo tsopano ife tikumva kuti Mbewu ya Abrahamu sinali mbewu yeniyeni ya kugonana kudzera mwa Sarah, amene anali Isaki, amene anapanga fuko, koma Mbewu yachifumu inali mwa lonjezo, amene anali Yesu Khristu. Ndipo kudzera mu Mbewu imeneyo, Iye anadzutsa Mbewu yachifumu. Oh, mai! Tsopano ife ndife ansembe achifumu, mtundu wachifumu, mtundu woyera, kupereka matamando kwa Mulungu, nsembe ya milomo yathu kupereka matamando kwa Dzina Lake. Mulungu anatsimikizira Mawu Ake, Iye anatsanulira Mzimu Woyera pa ife.

138 Iye anati, “Monga zinakhallira mmasiku a Sodomu, chomwechonso izo zidzakhala mu tsiku limene Mwana wa munthu ati adzaululidwe.” Tsopano kodi inu munazindikira? Kuchokera kwa Mwana wa Mulungu, Iye asanadzakhale Mwana wa Davide, Iye akudziulula Yekha kenanso ngati Mwana wa munthu. Kodi inu munazindikira Lembalo?

139 Pakuti, Iye nthawizonse amatero, Iye samachita kalikonse pokhapokha Iye atadziwitsa icho kwa antchito Ake aneneri. Ndizo ndendende. Ndicho chimene lonjezo Lake linali. Mukuona? Iye samachita kalikonse. . . Mulungu sanganame. Iye nthawizonse amaulula izo, koyamba, Iye asanachite izo.

140 Tayang’anani chochitika chimene ife tikukhalamo lero. Taonani pamene ife tiri. Aliyense wa inu muvomereza kuti tiri mu Sodomu wamakono. Inu mukudziwa kuti dziko lino likupanga izo. Pali. . . kupitirira chiyembekezo; palibe chipulumutso chatsalira kwa fuko lino kapena fuko lina. Ife tapyola zimenezo tsopano. Maulosi amene analosera za izi, akwaniritsidwa. Mulungu akukunkha, akuitenga nkhosa yaing’ono yotsiriza ija kulikonse kumene iyo ili. Zonse zidzalowa, tsiku lina. Ife tiri kumapeto a nthawi. Tayang’anani, mwa pamalo.

141 Ine ndikukupemphani inu, basi monga m’bale kapena mlongo, kuti mumange mphindi yokha ya chikhulupiriro ife tisanawapempherere anthu awa. Ndipo ndikudziwa kuti sitikuyenera kupita nthawi inayake. Koma ine—ine—ine ndikufuna kuti ndiyambe mzere wa pemphero, ndiye inu amene mukuyenera kuti mudzipita mupite ndiye. Mukuona? Inu amene mukufuna kukhala mu mzere wa pemphero mukhoza kutsalira.

Koma mungondirola ine, monga m'bale, ndingokulozerani inu chinachake kwa mphindi.

¹⁴² Muwoneni Yesu, mu Luka 17:30, taonani, pamene Iye ankanena pamenepo za mapeto a nthawi, momwe iwo akanati adzakhalire mmasiku a Nowa. Kenako Iye anati, “Ndipo monga, momwemonso, mmasiku a Sodomu,” anati, “pamene Mwana wa munthu azidzaululidwa.” Mwana wa munthu kenanso, osati Mwana wa Mulungu. “Mwana wa munthu,” mwaona, izo zikubweretsa Malaki 4 kenanso, molunjika kumene mmbuyo. Mauneneri ena onse awa akubwera momwemo, momwe izo zikuyenera kuchitikira. Iye amatsimikizira Mawu Ake kuti ali chomwecho. Uko nkulondola.

¹⁴³ Ndipo zindikirani, pakuchita chomwecho, momwe Iye ati adzatsanulire Mzimu Wake pa mnofu wonse, ndi chimene chiti chidzachitike, momwe kubwezeretsa kudzabwerere. “Ndipo ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera. Pa adzakazi Anga ndi antchito Ine ndidzatsanulira Mzimu Wangwa. Ndipo Ine ndidzawonetsera zizindikiro mmiyamba.”

¹⁴⁴ Ine ndiri ndi chithunzi apa, cha M'bale Lee Vayle pano. Ine ndikufuna ndikuwonetseni inu basi chimene chinachitika kuphiri, tsiku lina, pamene ana asukulu onse anadzatuluka panja, basi lisanati phunziro lalikulu ili la kutsegula, Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiwi zimenezo. Pamene ana asukulu anadzatuluka panja, ndinali pamwamba apo ndikupemphera, apa panali Moto uli monga nguli ukutsika, kenako nkubwerera mmwamba nkukaphulika, ndi kutembenuka ndi kudzabwerera pansi kenanso. Ndicho chimene Iye ananena choti ndipite ndikawauze anthu. Ife. . . Ndi Izo apo, kumene masukulu aku Tucson. . . ndi kumene Iwo unapita mmwamba mlengalenga.

¹⁴⁵ Ndipo sayansi inajambula zithunzi, ndi zina zotero, ndipo anafunsa za Izo. Iwo anati, “Kodi Izo ziri kuti? Chinachitika ndi chiyani?” Iwo sangathe kuzimvetsa izo, mwaona. Oh, izo sizinachitikire pakona, zinangodetsa chikumbumtima basi. Izo sizinati. . . Yesu, pamene Iye anali kuno, panali mamillioni a anthu sanadziwe kuti Iye anali pa dziko lapansi. Eya. Padzakhala mamillioni lero amene sadzamvetsa, ma teni a mamillioni a iwo.

¹⁴⁶ Koma kudzakhala, kwa iwo Amene Izo zinatimizidwako, iwo adzamvetsa. “Anzeru adzamudziwa Mulungu wawo tsiku limenelo, ndipo iwo adzachita zazikulu.” Ife tikuzindikira zimenezo, ora limene ife kukhalamo tsopano.

¹⁴⁷ Yang'anani pa Sodomu tsopano, onani chimene chinachitika. Iye anati, “Monga zinali mmasiku a Sodomu.” Panali gulu la anthu limene linkafunafuna mwana wolonjezedwa. Ife timakhulupirira zimenezo. Ameneyo anali Abrahamu ndi gulu lake. Apo panali gulu lofunda, Loti, wobwerera mmbuyo

mwatheka, komabe wokhulupirira; uko mu Sodomu. Magulu atatu a anthu.

¹⁴⁸ Nthawizonse pamakhala magulu atatu amenewo. Hamu, Shemu, anthu a Yafeti. Ndiponso, okhulupirira, odzipangitsa kukhulupirira, ndi osakhulupirira. Iwo amapezeka konsekonse, ndipo ife—timawapeza iwo mu gulu lililonse. Ndipo, kulikonseko, inu mumawapeza iwo. Ndipo magulu amenewo akadali kuno. Mukuyenera kugawa izo. Inu mukhoza kuzitenga izo kudutsa mu Lemba, zimangodzilumikizira zokha mkati momwe.

¹⁴⁹ Mvetserani kwa ichi. Yang'anani pamene ife takhala, mwamalo ndi mwauneneri, usikuuno. Tsopano, aliyense wa ife akudziwa kuti dziko liri mu chikhalidwe cha Chisodomu.

Ife tikudziwa mauneneri onse a Israeli, ali mu dziko la kwawo. Ngati inu mukufuna kudziwa mwadziko pamene ife taima, muyang'ane Israeli, kumene iye ali.

¹⁵⁰ Ngati inu mukufuna kudziwa chikhalidwe chimene mpingo uli, muyang'ane momwe akazi akuchitira. Iye ndi mpingo. Kumuona iye, wachigololo, wopanda ulemu; penyani, onani pamene mpingo uli. Mungopenya izo, mwaona, mwaona, mungowayang'ana akazi. Inu mwaona pamene, momwe akazi anu akunyozekera ndi kukhala oyipitsidwa kwambiri, umo ndi momwe mpingo wanu uliri, mwaona, choyimira.

¹⁵¹ Yang'anani kumene Israeli ali, inu muwona chithunzi cha nthawi pamene ife tiri. Mwaona, mungopenya zizindikiro zimenezo ndi zodabwitsa. Ngati inu—ngati inu, kapena ngati maso anu ali otseguka, muwona pamene ife tiri.

¹⁵² Tsopano penyani mwapamalo pamene ife takhala, dziko mu chikhalidwe cha Sodomu. Tsopano zindikirani, “monga izo zinali.” Tsopano zindikirani, panali winawake, mu tsiku limenelo, akuyembekezera mwana wolonjzedwa wakudza. Abrahamu ndi Sarah, iwo anali akuyembekezera mwana wolonjzedwa mu gulu la Abrahamu. Iwo sanali mu Sodomu. Koma basi pa nthawiyo, mutu womaliza wa chochitikacho, basi mwana wolonjzedwayo asanabwere, panali amuna atatu amene anabwera pansi kuchokera Kumwamba, Mngelo... Angelo awiri ndi Mulungu. Ndipo iwo anatsika ndipo anadzayankhula ndi Abrahamu, pansi pa mthundu. Nkulondola uko? Ndipo awiri a iwo anapita ku Sodomu ndipo anakafuula motsutsa machimo a mzindawo. Ndipo izo zinali basi kusanachitike kuwotchedwa kwa dziko la Amitundu, pa nthawi imeneyo. Sodomu yense anawonongeka pomwepo. Ochepa okha anatulutsidwako, Loti ndi ana ake aakazi awiri. Mkazi wake sanakwanitse nkomwe; iye anatembenukira mmbuyo. Momwe ine ndikanakondera ndikanakhala nayo nthawi kuti ndikuwonetseni inu zimenezo pakali pano, pamene mpingo umenewo wayima pa malo amenewo. Ine ndikufuna inu muzindikire tsopano.

153 Ndipo Munthu mmodzi anatsalira mmbuyo, amene anayankhula kwa Abrahamu, ndipo Iye anachita chizindikiro kwa Abrahamu. Ndipo, penyani, Abrahamu anali atamuwona Mulungu mu zizindikiro zazikulu zambiri. Ife timakhulupirira zimenezo, si choncho ife? Mwana wobwerayo asanafike. Koma mwanayo asanawonetseredwe, panali chizindikiro chimene iye anapatsidwa.

154 Chifukwa, Mwana, Mwana woona, an kayenera kuti adzakhale Mwana wa Mulungu, kudzera mu chikhulupiriro cha Abrahamu, mwaona, anali Yesu. Ife pokhala mbewu ya Abrahamu, akufa mwa Khristu, timadzakhala mbewu ya Abrahamu.

155 Zindikirani tsopano izo zisanachitike, mwana uyu woti abwere. Tsopano, Mmodzi uyu amene anakhala ndi kumayankhula ndi Abrahamu, anali atatembenezira nsana Wake ku hema, ndipo Iye anati, "Abrahamu." Tsopano, basi tsiku zisanachitike zimenezo, iye anali Abram. Tsopano Iye anati, "Abrahamu, ali kuti mkazi wako, Sarah?" osati Sarra, S-a-r-r-a. S-a-r-a-h, mfumukazi. "Ali kuti mkazi wako, Sarah?"

Anati, "Iye ali mu hema kumbuyo Kwanu."

156 Iye anati, "Ine ndidzakuhezera inu, mwaona, molingana ndi lonjezo Langa limene Ine ndakupangirani inu." Mwakulankhula kwina, "Nthawi ya moyo, Sarah adzayamba mu nthawi yake ya wamba ya moyo kenanso."

157 Ndipo Sarah, pokhala wokalamba, usinkhu wa zaka handirede tsopano, ali mu hema, anaseka mwachinunu. Mwaona, iye anamwetulira kwa iyemwini, anati, "Munthu ameneyo angakhale wolondola bwanji? Mwaona, ine mkazi wokalamba, mbuye wanga Abrahamu kunja uko, nayenso wokalamba, zochitika za pabanja zinali zitatha kwa zaka." Anati, "Ndingakhalenso ndi kusangalala bwanji ndi mbuye wanga? Iye pokhala wokalamba, ndipo ine wokalamba, wopitirira kubereka, mitsempha ya mkaka inapita, chirichonse... 'Iye ndi wouma.' Kodi ife tingakhalenso bwanji ndi chisangalalo?"

158 Ndipo Mmwamuna uja, atatembenezira nsana Wake ku hema, anati, "Nchifukwa chiyani Sarah anaseka, akuti, 'Kodi zinthu zimenezi zingatheke bwanji?'" Chimenecho chinali chiyani? Kuzindikira za mu mtima, uneneri! Mukuona? Mukuona? Icho ndi chimene iye anachiwona.

159 Tsopano Iye anati, "Ameneyo adzabwereranso, ndipo Mwana wa munthu," chimene icho chinali, ameneyo anali Mwana wa munthu pamenepo. Chabwino, anamutcha Iye Elohim, "Ambuye Mulungu." Elohim, aliyense akudziwa kuti ndiko kulondola, Elohim ndi Ambuye Mulungu. "Pachiyambi Elohim analenga miyamba ndi dziko lapansi," Mmodzi wokwanira muzonse. Mwana wa munthu wosandulika thupi,

apo Iye anali atayima pamenepo mu thupi pa nthawi imeneyo, ngati fiofane, atayima pamenepo akuzindikira chimene Sarah ankanena mu hema kumbuyo kwa Iye. Iye analonjeza. Penyani. Mbewu Yachifumu ya Abrahamu yalonjezedwa kuti idzawona chinthu chomwecho.

¹⁶⁰ Koma zindikirani Loti, iye anali ndi mtumiki kumusi uko, nayenso, awiri a iwo anapita kumeneko. Mmodzi wa iwo anapita kumusi uko, ndipo wina anapita kumusi ndi iye, ndipo iwo anakalalikira ndipo anawaitana anthu kuti athawe ku mkwiyo umene unali nkudza.

¹⁶¹ Mwapamalo, dziko silinakhalepo mu chikhaliidwe chimenecho, kuyambira tsiku lija limene Yesu anapanga lonjezo, mpaka pano. Ine ndikufuna kumufunsa wa zambiriyakale aliyense amene angakhale ali mchipinda chino, kapena ngati inu mudzamve ngakhale pa tepi iyi, ndi kudzamva izo pa nthawi iliyonse, chonde dzandilembereni ine. Ndaphunzira mbiriyakale tsopano kwa zaka sarte, mbiriyakale ya Baibulo, ndipo sipanayambe pakhalapo munthu amene ine ndinayamba ndamuwonapo mu mbiriyakale yonse ya mpingo, kupyola mu mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo. Kutu ife tsopano tiri mu Laodikaya, ndipo ife tikudziwa zimenezo.

¹⁶² Sipanayambe pakhalapo mtumiki, amene anayamba wapitapo ku mpingo wonse, wa dzina lake lothera ndi h-a-m, mpaka pano. G-r-a-h-a-m, Billy Graham. Pakhala pali a Moody, Finney, Sankey, Knox, Luther, ndi ena otero, koma osati h-a-m, “atate wa mafuko.” Tsopano kumbukirani, iye ndi G-r-a-h-a-m, zilembo sikisi. Koma A-b-r-a-h-a-m ndi zilembo seveni. Zindikirani, iwo ali kumusi uko, Billy Graham, akupita mu—madera onse a dziko lapansi, ndi kuyitanira kutuluka mu Sodomu, “Tulukani, thawani mkwiyo umene ulinkudza.” Palibe munthu amene ine ndikumudziwa, kumundako, amene wamugwira Mulungu, pa mawu amenewo a kulungamitsidwa, monga Billy Graham amachitira. Iye akhoza kuchipereka icho. Iye si wazaumulungu wotero...ine ndikuganiza kuti iye ndi wazaumulungu, koma iye si mphunzitsi wamphamvu. Koma Mulungu ali naye iye. Mwamuna ameneyo amayima pamenepo ndi ngati phunziro la Sande sukulu, nkuwagwira anthu amenewo ali kakasi. Iyeyo ndi wantchito wa Mulungu wa ora lino. Kwa ndani? Mpingo wachibadwa, umene uli mu Sodomu.

¹⁶³ Koma kumbukirani, panali mpingo umodzi wauzimu, umene sunali mu chovala chachipembedzo chimenecho, ngakhalenso. Gulu loyitanidwa atuluke, ndipo iwo analandira uthenga, nawonso, ndi wa mthenga. Ndipo icho chinali chiyani? Kuzindikira maganizo amene anali mu mtima. Mulungu nthawizonse amatsimikizira Mawu Ake.

¹⁶⁴ Tiyeni tipemphere. Okondedwa Atate Akumwamba, nthawi

yofunikira iyi, pamene ziganizo zikuyenera kupangidwa, nthawi ikudutsabe, ife sitikudziwa ora limene Ambuye wathu angabwere. Ndipo pamene ife tikuwona mauneneri awa amene apangidwa ndi Iye, kudutsa mwa aneneri Anu kudutsa mu mibadwo, tsopano akufutukuka. O Mulungu, momwe ine ndikukuthokozerani Inu chifukwa cha izi, kuti ngakhale mwamuna wa thupi lothekera, mwamuna wothekera mu—mu zaumulungu, amene angathe kuyima motsutsa zinyengo za dziko ndi osakhulupirira, ndi pa magulu awa, ndi kudutsa mthunzi wa kukayikira ayima pamenepo molimbika ndi olimba mtima, akudziwa pamene iwo ayima ndi kutsimikizira Mawu amenewo kuti ndi owona, mwa Malemba. Ndipo kenako ife amene tikuyembekezera Kudza Kwanu, Ambuye, tikukhulupirira zinthu zina izi zimene zinaloseredwa kuti zikanadzachitika, kuyima ndi kusangalala kukuwonani Inu mukuyenda pakati pathu ndi kuchita chinthu chomwecho chimene Inu munati chidzakwaniritsidwa, kutsimikizira Mawu Anu kuti ndi owona. Mulungu Wamuyaya, ana Anu odwala akhala apa.

¹⁶⁵ Ine sindikudziwa kuti tiri ndi nthawi yochuluka bwanji yogwira ntchito. Dzuwa lamadzulo likumira. Koma Inu munalonjeza, kwa mneneri, “Kudzakhala Kuwala pa nthawi ya kumadzulo.” Ndipo ife tikuwona dzuwa lomwelo likutuluka kummawa, ndi ilo limene likudzalowa kumadzulo. Chitukuko chayenda ndi dzuwa ndipo tsopano ife tiri ku Gombe la Kumadzulo, ndipo Uthenga wayenda ndi chitukuko. Tsopano, Atate, ife tikudziwa kuti awa ndi mathero a Uthenga, mapeto a nthawi, mapeto a m’badwo. Iwo ukuzimirira mu Muyaya. Koma Inu munalonjeza kuti Mwana adzatulukira, Mwana wa munthu adzaululidwa. Mmasiku otsiriza, izi zikanadzachitika. Kuwala kwakumadzulo kwabwera, Atate. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha izo. Ndipo modzichepetsa momwe izo ziliri, komabe Inu mumachita izo mophweka, nthawi zambiri, kuti izo zimapita pamwamba pa opambana, otchedwa oganiza mwakuya, ndi kuwulula izo kwa makanda omwe ati aphunzire.

¹⁶⁶ Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu muzipanga izo chomwecho, usikuuno, kuti ana Anu osawuka odwala pano awone lonjezo la Mulungu, ndipo mmodzi aliyense wa iwo achiritsidwa, ndipo adzatuluka muno, mawa, ndi matupi amphamvu atsopano, ndi kukhala abwino kenanso. Perekani izi, Ambuye, kuti iwo athe kutenga Uthenga kuchokera kwa wina kupita kwa mzake, mpaka wotsirizayo atalowa mu khola, ndipo kenako zitseko zidzatekedwa. Tithandizeni ife, wokondedwa Mulungu. Ine ndikukupemphani Inu, usikuuno, mu nkhope ya zonsezi, ngati Inu mungatero kamodzinsu, Atate, chifukwa cha ine.

¹⁶⁷ Izo—izo zimawoneka, usiku wina, anthu sanazizindikire izo mochulukuka. Koma, ine ndikupemphera, mulole izo zichitike kenanso usikuuno, Ambuye. Chifukwa, ndadutsitsa nthawi

yanga yoti ndiyankhule, koma ine sindikudziwa kuti tikhala ndi nthawi yayitali bwanji kuti tichite izi. Chotero, ine ndikupemphera, Atate, kodi Inu mundimva ine? Ndipo kumva pemphero la amuna aumulungu awa ndi akazi amene akhala pano usikuuno, amene ali odzazidwa ndi Mzimu Wanu. Iwo ndi okhulupirira, Ambuye, Inu mukhoza kungogwira ntchito pakati pawo. Ndipo ndife. . . Ine ndikupemphera kuti Inu mutsimikizire Mawu Anu amene Inu munawanena, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iye adzazichitanso.” Mulole izo zikhale kenanso, Yesu, kuti atsimikizire kuti Inu ndi yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ine ndikupempha izi kwa ulemelero wa Mulungu, mu Dzina la Mwana Wake, Yesu Khristu. Amen.

¹⁶⁸ Tsopano, kwa mphindi yokha, ine ndikufuna ndidziwe ndi anthu angati muno amene ali ndi makadi apemphero. Ine—ine ndikufuna inu mukweze manja anu, aliyense wa inu amene muli ndi makadi a pemphero. Chabwino, ndi zachidziwikire, ine ndikuganiza, pafupifupi paliponse.

¹⁶⁹ Ine ndikudabwa ndi anthu angati muno amene alibe makadi apemphero, ndipo komabe inu mukudwala, kodi mungakweze manja anu ndikuti, “Ine ndiribe khadi la pemphero, ndipo komabe ine ndikudwala. Ndine wosowa.”

¹⁷⁰ Ine ndikufuna ndikufunsi inu kuti mukhale olemkeza kwa kanthawi. Tsopano, ine ndimakonda kuyankhula nanu. Limenelo ndi vuto langa nthawizonse, ine ndimayankhula motalikitisa kwambiri. Koma inu musanabwera, ine—ine ndikuyembekeza ndi kudalira kuti Mulungu atsimikizira izi ndipo chimene ine ndanena kuti ndi Choonadi, ndi kumulola—kumulola Iye angowona.

Tsopano, ndi angati akhala kunja uko amene akudwala, amene akudziwa kuti ine sindikudziwa chinthu chimodzi chokhudza inu, kwezani mmwamba manja anu. Tangoyang’anani pa izo. Chabwino.

Ine ndikufuna inu opanda makadi apemphero tsopano. Makadi apemphero ayitanidwa. Ine ndikufuna kuti inu mupemphere.

¹⁷¹ Baibulo linanena kuti, “Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Iye akuti, “Iye ndi Wansembe Wamkulu wakhalani pamenepo akupanga kupembedzera pa kuvomereza kwathu.” Tikuyenera kuvomereza izo poyamba, Iye asanakhale Wansembe Wamkulu, chifukwa Iye amangopembedzera ku kuvomereza kwathu. Nkulondola uko, abale otumikira? Mwaona, Iye amangopembedzera pa kuvomereza kwathu, chimene ife tikuyomereza kuti Iye ali, chimene Iye watichitira ife. Osati chimene Iye *ati* adzachite. Iye wachita kale izo. Iye tikuyenera kuvomereza kuti Iye wachita

izo. “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.”

¹⁷² Tsopano, Atate Akumwamba akudziwa. Ndipo kuyang’ana pa inu, ndi kuwona ine ndamzindikira mzanga wabwino wochokera ku Ohio, iye ndi mkazi wake akhala apa, ndi Bambo Dauch ndi mkazi wake. Ndipo ine ndikukhulupirira, wakhala pachiwiri kapena pachitatu kuchokera kwa iwo, ndi kenanso M’busa uja, Bambo Blair amene ndinamuona usiku watha. Kuli mdima pa omvetsera, kwa ine, chifukwa cha magetsi awa pano ndi mdima pang’ono kwa ine, ndipo ine—sindikukuonani inu bwino kwambiri.

¹⁷³ Koma ine ndikufuna kuti inu mupemphere. Ndipo muyike pamtima panu chimene mukufuna, ndipo mumupemphe Wansembe Wamkulu wathu, Amene akhoza kukhudzidwa ndi zowawa zathu.

¹⁷⁴ Tsopano, ine posakudziwani inu, ndipo inu mukhoza kungondikhudza ine paliponse, kukhala ngati mukukhudza m’bale wanu, mwamuna wanu, abusa anu, winawake, izo sizinga—sizingachite bwino. Koma ngati mungamukhudze Iye, ndipo ngati ife tikukhala moona ndi Mzimu Wake, ndiye Iye akhoza kugwiritsa ntchito chikhulupiriro chanu kuti mumukhudze Iye, ndi mphatso yanga kuti ndiyankhule mobwereza.

¹⁷⁵ Mwaona, ine ndikanakhala wosayankhula monga ichi, ichi chiri *apa*, chopanda liwu kuyankhula kupyolera mwa icho. Pakuyenera kukhala . . . Ichi, ichi ndi chosayankhula pakakhala popanda chinthu apa choti chiyankhule kudzera mwa icho. Ndipo chomwechonso munthu aliyense, ndi wosayankhula, pamene zifika kwa zinthu izi, pokhapokha ngati Mulungu ayankhula kudzera mwa iwo.

¹⁷⁶ Tsopano inu mupemphere, ndipo tiyeni tiwone ngati zinthu izi zimene ine ndanenazi ziri zoono. Mulungu athandize kuti zikhale chomwecho. Ine sindikunena kuti Iye atero. Ine ndikuyembekeza kuti Iye atero. Ine ndikudalira kuti Iye atero. Iye sanandikhumudwitsepo ine, kwa zaka zambiri, kudutsa ndi kuzungulira dziko lonse lapansi, ndi mitundu yonse ya mafuko, ndi mamillioni a anthu. Iye sanandilepherepo ine. Ndipo ine ndikutsimikiza, motsimikiza basi monga ine ndikukhulupirira kuti ndaima pano, Iye sandilephera ine tsopano.

¹⁷⁷ Ine ndikufunsani inu kuti mukhale olemekeza ndipo mukhale pansu, kwa mphindi zochepa chabe. Ife tibalalitsa gulu lomvetsera lalikululi ndi kupempherera odwala, mu mphindi chabe.

¹⁷⁸ Koma ine ndikufuna inu, inu okhulupirira, kuti ngati inu mungati musayang’ane kwa ine, koma kukhulupirira. Ndikuti, “Ine ndikukhulupirira kuti chimene munthuyo wanena ndi Lemba. Ine sindikudziwa momwe ife tiri kutali mu nthawi

monga iye amati ife tiri. Koma, ngati izo ziri, ndiye zikuyenera kuchitika. Ngati Mawu ake ali Mawu a Mulungu, ndiye, mawu ake adzalephera koma Mawu a Mulungu sadzalephera.”

¹⁷⁹ Mulungu ndi wokakamazika kuchirikiza Mawu Ake. Iye adzawatsimikizira Iwo. Iye adzawatsimikizira Iwo. “Iye amene akhulupirira pa Ine.” Iye anatsimikizira kuti ili ndi tsiku lomaliza. Iye anatsimikizira chimene chikanadzachitika. Iye anatsimikizira kuti ichi chikuyenera kuchitika.

¹⁸⁰ Ndipo, kumbukirani, Abrahamu ndi gulu lake sanalandire konse chizindikiro chinanso kuchokera kwa Mulungu, mpaka mwana wolonjezedwayo atafika. Ndi angati akudziwa kuti izo ndi zoono? Chizindikiro chija cha kuzindikira za mumtima! Ndipo Mbewu yachifumu ya Abrahamu, ndiroleni ine ndikumveni inu. . . Ndiroleni ine ndikuuzeni inu, PAKUTI ATERO AMBUYE, inu mukulandira chizindikiro chanu chotsiriza. Ndizo mogwirizana ndi Malemba ndi vumbulutso la Mulungu limene liri mu mtima mwanga, limene likunena kuti ichi ndi Choonadi. Ndipo ine ndikudalira kuti inu mukukhulupirira izo kuti ndi Choonadi.

¹⁸¹ Tsopano inu mukhulupirire. Aliyense amene akungokhulupirira, anene, “Ambuye Yesu, ndiroleni ine ndikugwireni Inu. Ine ndiri ndi chosowa mu mtima mwanga, ndipo ine ndikudziwa M’bale Branham sakudziwa kanthu za ine. Ine sindikumudziwa nkomwe mwamunayo, iye sakundidziwa ine, koma Inu mukudziwa. Ndipo ngati iye wandiuzwa ine Choonadi, izi zichitika.” Ine ndikukufunsani inu, musasunthe tsopano, basi kwa kanthawi pang’ono. Khalani kwenikweni. . .

Mwaona, ndinu mzimu. Ndipo ine ndikutengera mzimu uliwonse muno pansu pa ulamuliro wanga, mu Dzina la Yesu Khristu, kuti Mawu Ake akhoze kukwaniritsidwa.

Tsopano mungokhala molemekeza. Pempherani. Muyang’ane kwa Iye, ndikuti, “Ambuye, ine ndikukhulupirira izo. Muthandize Inu kusakhulupirira kwanga.”

Tiyeni tiyambe. Ine ndikuyenera kukhazikika pa chinachake cha gawo la chipindachi apa, chifukwa, mwaona, ambiri a inu, ndipo aliyense wa inu ndi mzimu.

¹⁸² Ine sindingathe. Inu mukuti, “Nanga bwanji ine?” Sindingathe kukuuzani inu. Izo ndizochita pazokha. Ntchito zonse za Mulungu ndi zochita mwazokha. Pakhala anthu ambiri ochiritsidwa akudutsa pa nsanja ino, usikuuno, mwinamwake padzakhala ambiri amene satero. Zonsezo ziri mu kuchita kwayekha kwa Mulungu. Ndani angamuuze Iye choti achite? Palibe aliyense. Iye amagwira ntchito mogwirizana ndi chifuniro Chake Chomwe, dongosolo Lake Lomwe.

¹⁸³ Koma inu mungokhulupirira. Mukhale odzichepetsa. Musakhale wamanjenje. Ingofikirani kwa Mulungu ndi kuti, “Ambuye Mulungu, ine ndikukhulupirira izo.” Mukuona?

“Ndiroleni ine ndikhudze chovala Chanu. Ine ndikusowa *chakuti-ndi-chakuti*. Ndikudziwa kuti m’baleyo samandidziwa ine kapena kudziwa chosowa changa, koma iye anatiuza ife za zinthu izi zimene Inu munachita, ndi kunena kuti Inu muli pano yemweyo lero.”

¹⁸⁴ Izo sizikupatula abale inu pano pa nsanja, aliyense wa inu. Ine ndikungokufunsani inu, abale anga, monga antchito amzanga a—a Uthenga wa Khristu. Ine ndikuyankhula kwa inu moona mtima basi monga ine ndikudziwira, monga a—munthu wakufa ndi inu, mwaona, akusiya dziko lino. Ife tikuyenera kuchokapo. Ndipo ndidzayenera kudzayankhira pa Tsiku la Chiweruzo, pa chimene ndikunena. Ine ndikudziwa za zimenezo, ndikudziwa kwambiri. Ndipo ine ndikukuyamikira iwe mwamuna, chimene iwe uli, waima pano ndi ine, kundithandizira ine. Ine ndikuyesera kuti ndikuthandizeni inu, kuti ndichite chirichonse chimene ine ndingathe, chifukwa cha Ufumu wa Mulungu.

Ine ndikupemphera ndi kufunsa.

Pano, ndi angati anayamba awonapo Kuwala uko pa chithunzi? Inu munachiwona chithunzi cha Iko? Apo Iko kwapachikika pomwe apo. Kodi inu simukuona Iko?

¹⁸⁵ Iko kuli pamwamba pa dona uyo amene wakhala apo ndi mpango wake. Iye akumupempherera wokondedwa wake. Uko nkulondola, dona. Wokondedwa ameneyo... Kodi iwe ukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake, kapena mundikhululukire ine, wantchito Wake? [Mlongo akuti “Ine ndithudi ndikutero.”—Mkonzi]. Iwe ukukhulupirira zimenezo? Chabwino. Tsopano, ngati Mulungu angaulule kwa ine chimene chiri cholakwika, bwanji, iwe uvomereza kuti izo zikuchokera kwa Mulungu, monga ngati mkazi amene anakhudza chovala Chake? Tsopano, iwe ukudziwa uli—uli mapazi twente kapena sarte kuchokera kwa ine, kapena kupitirira, iwe sunandikhudze ine nkomwe. Koma iwe wakhudza Chinachake, chimene iwe ukudziwa kuti walumikizana nacho Chinachake, Winawake. Chimene icho chiri, ndi cha mkazi, amene ndi mwana wako wamkazi. Uko nkulondola. Kodi ukukhulupirira kuti achiritsidwa? Iye ndi chidakhwa cha zoledzeletsa. Uko nkulondola ndendende. Ine ndikumuona iye akusambira, ataledzera. Mukuona? Tsopano, mpango umene iwe uli nawo mdzanja lako, iwe ukawuike pa iye, ndipo usakaikire. Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu amuwombola iye. Kodi ukhulupirira izo ndi ine? Amenii.

Tsopano, ine sindikumudziwa mkaziyo, koma Mulungu akumudziwa iye. Kodi iwe ukukhulupirira tsopano ndi mtima wako wonse?

¹⁸⁶ Mwamuna wakhala pamwamba apo atavala malaya amizeremizere, ali ndi chotupa, iwe ukukhulupirira kuti

Mulungu akuchiza iwe ndi kukupanga iwe kukhala bwino? Kodi iwe ukukhulupirira kuti Iye achita izo? Ine sindinayambe ndamuwonapo mwamunayo mmoyo wanga. Inu muli ndi khadi la pemphero, bwana? [M'baleyo akuti, "Ayi, ine ndiribe."—Mkonzi]. Inu mulibe? Inu simuikusowa iyo.

"Ngati inu mungakhulupirire!"

¹⁸⁷ Apa pakhala mkazi akuyesera kuyang'ana pamwamba pa mkazi uyu wakhala apa. Iye ndi mlendo kwa ine. Koma iye ndi wamanjenje kwenikweni. Ine sindikumudziwa iye. Ine sindinayambe ndamuwonapo iye, mmoyo mwanga. Koma Mulungu akumudziwa iye, ndipo iye akuzindikira pakali pano kuti iye akulumikizana ndi Chinachake. Iwe wakhala ukupemphera pamenepo pa chifukwa china. Chifukwa chimene iwe uliri, iwe sungakhale motalikirapo kuposa usikuuno. Iwe ukuyenera kuchoka pa msonkhano. Iwe ukukonzekera zopita kwanu, mawa. Iwe siwochokera kuno, kapena iwenso siwochokera ku California. Ukupita kummawa ukachokera pano. Ukupita pa ndege. Iwe ukukonzekera, kupita pa ndege. Ndiwe wochokera ku Oklahoma. Eya. Uko nkulondola.

¹⁸⁸ Iwe ulinso mu chochitika chakufa. Iwe unabwera kuno kuti udzapemphereredwe. Iwe ulibe khadi la pemphero. Koma iwe unakhulupirira kuti uchiritsidwa, ngati iwe ungabwere kuno. Uko nkulondola. Komanso, vuto lako ndi khansa. Khansa ili mu fupa. Iwe ukukhulupirira kuti uchiritsidwa tsopano? Iwe ukukhulupirira kuti walumikizana ndi Iye, mlongo wanga? Mwinamwake Mulungu andiiza ine yemwe iwe uli, ndiye izo zingakuthandize iwe? Ngati ndi choncho, kweza mmwamba dzanja lako ngati ukukhulupirira izo, kuti (Mulungu) izo zikuthandiza iwe. Chabwino, Akazi a Steel, mukhoza kubwerera ku Oklahoma.

Ine sindikumudziwa donayo. Ine sindinayambe ndamuwonapo iye.

¹⁸⁹ Apa pali dona wakhala kumbuyo komwe kuno kuseri kwa iye. Iye akuvutika ndi mitsempha yotupa. Ndipo iye alinso ndi mwana wamwamuna amene ali chidakhwa, ndipo iye akumupempherera iye. Ngati iye ati akhulupirire, iye akhoza kuchiritsidwa. Akazi a Mason, kodi inu mukhulupirira ndi mtima wanu wonse, ndi kukhulupirira kuti Yesu Khristu apereka machiritso kwa inu? Inu mukutero?

Chabwino, ndiye ikani dzanja lanu pa dona amene wakhala pafupi ndi inu pamenepo, iye akumupempherera mwamuna wake amene sanapululumutsidwe. Mulungu apereka machiritsowo.

Tiyeni tipemphere.

¹⁹⁰ Wokonedwa Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mupereke mdalitso umenewo kwa iye. Mumpatse mkazi ameneyo chokhumba cha mtima wake, Ambuye. Chikhulupiriro

chake chiri pafupi kwambiri kwa Inu, icho chakukhudzani Inu. Ndipo ine ndikupemphera, Atate, kuti Inu muthandize, mu Dzina la Yesu. Amenii.

Tsopano mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, kuti mulandira izo. Inu muchita zimenezo? Chabwino. Mulungu akudalitseni inu.

Kodi iwe ukukhulupirira kuti mwamuna wako apulumutsidwa, dona? Kodi iwe ukukhulupirira ndi mtima wako wonse? Kweza mmwamba dzanja lako, iwe utero.

¹⁹¹ Zikuwoneka kuti pali, pamaso panga, mkazi amene ali wolemera kwambiri. Apo iye wakhala. Iwe ukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito wa Mulungu? Iwe ukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito wa Mulungu? Iwe ukutero. Chabwino. Ine sindikukudziwa iwe. Chimene vuto lako liri, ndi zokhudzira. Ndiwe wonenepa kwambiri. Iwe wakhala uli kwa adokotala, iye anati iye sangachite kanthu za izo, koma ameneyo anali dokotala wapadziko lapansi. Mukuona? Ako...Iwe unangokhala ndi chisoni chochuluka. Wataya mwamuna wako. Iwe si wochokera kuno. Iwe kwenikweni ndiwe wochokera ku Arkansas. Ukufunafuna ntchito, aponso, ndipo sukuyipeza ntchitoyo. Iwe umawopa kuti, chinachake, iwe suyitanidwa. Koma chikhulupiriro chako tsopano chamukhudza Mulungu. Mlongo wanga, iwe zipita, ukukhulupirira. Mulungu akupatse iwe ntchitoyo, akupatse iwe chokhumba cha mtima wako.

Mulungu amatsimikizira Mawu Ake kuti ndi owona. Kodi inu mukukhulupirira izo kukhala chomwecho? Tsopano ine ndikungofuna kuti inu mupemphere ndi ine kenanso.

¹⁹² Atate Mulungu, Inu ndinu Mulungu yemweyo amene munatsimikizira. Pamene Inu munati, "Mtsikanayo sanafe, iye akugona," kenako Inu munkayenera kuti mutsimikizire zimenezo. Tsopano, Inu munalonjeza, kuti kudza kwa nthawi yotsiriza kusanafike, kuti Mwana wa munthu akanadzadziulula Yekha mwanjira yomweyo imene Iye anachitira ku Sodomu. Inu munalonjeza izo, Ambuye. Tsopano Inu mwabwera pa dziko lapansi, mmawonekedwe a Mzimu Woyera, ndipo mwadzafika pakati pathu, usikuuno, ife anthu okhulupirira, ndipo tatsimikizira izo. Inu mwatsimikizira Mawu Anu monga Inu munachitira tsiku lijali. Ambuye, sitikusowanso umboni. Inu muli pakati pathu. Ife timakukondani Inu. Ndipo ife tikuzindikira kuti ichi ndi chizindikiro chotsiriza Kudza Kwanu kusanachitike, molingana ndi Malemba. Ndipo mithunzi yonse ndi zoimira sizimalephera konse. Izo ziyenera kukhala zotsimikizika.

¹⁹³ Chotero ife tikupemphera, Atate, pamene ana Anu akubwera tsopano kuti adzapemphereredwe, kuti aliyense achiritsidwe. Mulole pasakhale munthu wodwala wotsalira pakati pathu, pa mapeto a msonkhano wa machiritso uwu. O Mulungu

wokonedwa, kodi Inu mungalole kudzoza Kwanu kukhale mwachisomo pa anthu Anu pakali pano, kuti mmodzi aliyense wa iwo achiritsidwe?

¹⁹⁴ Ndipo ngati pali ena pano, amene si ana Anu panobe, ndi pa maziko a zinthu izi, kuti. . . Iwo amva Mawu ndipo awona chinthucho chikuchitika, ndendende basi kutsimikiziridwa kwa lemba, ndi Yemwe Inu muli ndi chimene Inu muli, kuti Inu muli pano.

¹⁹⁵ Ndipo, Ambuye, kodi Inu munga—Inu mungadalitse bodza? Bwanji, ayi ndithudi, Ambuye. Koma Inu munalonjeza kuti mudzadalitsa Mawu Anu, ndipo Iwo sadzabwerera pachabe. Iwo adzakwaniritsa chimene Iwo analingaliridwa. Ndipo tsopano Inu mwachita zimenezo pamaso pathu, usikuuno, kupitirira mthunzi uliwonse wa kukaikira.

¹⁹⁶ Ndipo ndi mitu yathu yoweramitsidwa, kodi alipo anthu pano amene sanakhulupirirepo, amene angafune kungokweza dzanja lanu? Ndi mutu wanu woweramitsidwa, ingokwezani mmwamba dzanja lanu. Ndipo imani pa mapazi anu, ndi kuti, “Ine tsopano ndikukhulupirira, ndi mtima wanga wonse. Ndipo ine ndikufuna kuti ndimulandire Yesu Khristu, pakali pano.” Kodi inu mungachite izo, anthu aliwonse, anthu aliwonse amene ali pano, amene sanamulandirebe Khristu, ndipo mukufuna kuchita izo nthawi ino? Ine sindikuuzani inu. . . Inu muzipita ku mpingo umene mwasankha. Koma ine ndikukupemphani inu kuti mulandire Yesu Khristu pamene inu muli. . . Inu mwinamwake simudzakhala konse pafupi ndi Iye mpaka mutadzamuwona Iye mwa umunthu pamene Iye adzabwera mu thupi Lake lowoneka akuchokera Kumwamba. Kodi inu tsopano mumulandira Iye ngati simunachite kale izo?

¹⁹⁷ Powona kuti palibe amene waima pano, ine ndikukhulupirira ndiye kuti nonsenu ndinu oganiza bwino, anthu ozindikira, ndipo mukuzindikira chimene mukuchita. Ngati mwakhala pamenepo pansu pa ichi, inu mukumbukire, “Ngati inu mudzachita manyazi ndi Ine pamaso pa anthu, Ine ndidzachita manyazi ndi inu pamaso pa Atate Anga.” Panali winawake atayima, mwinamwake, inde, mwa omvetsera, kumbuyo uko.

¹⁹⁸ Wokonedwa Mulungu, iwo akhoza, ine sindikuwona, amene ayima, iwo akufuna kuti akulandireni Inu. Iwo akuzindikira, Ambuye, kuti izi sizinachitike mpaka nthawi ino, ndipo tsopano Inu muvomerezere izo ndi kutsimikizira kuti izo ziri chomwecho. Ine ndikupemphera, Atate, kuti mmitima yawo, izo zasunthidwa modabwitsa pa nthawi ino. . . Iye tingadziwe bwanji kuti mwina ameneyu ndi munthu womaliza kulowa? Awa akhoza kukhala mathero a Los Angeles. Uwu ukhoza kukhala moyo wotsiriza umene uti ubadwire mu Ufumu. Iye sitikudziwa pamene nthawi imeneyo idzabwere. Ndipo pamene

iyo idzatero, chitseko chidzatsekedwa, Thupi lidzakhala lathunthu. Ilo silidzakhala Thupi lopusa kapena Mkwatibwi wopusa. Ilo lidzangokhala ndi mamembala ochuluka kwambiri amene maina awo analembedwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, kumene Yesu anabwera kudzatenga, monga Adamu, anayenda kupita kukapululumutsa mkazi wake. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu muwalandire iwo tsopano mu Ufumu Wanu. Iwo ali mmanja Mwanu. Chitani nawo iwo, Ambuye, ine ndikupemphera mu Dzina la Yesu. Amenii.

¹⁹⁹ Mulungu adalitse aliyense wa inu amene munayima. Ine sindimadziwa kuti ena a inu munayima. Ena anaima kumbuyo, ena m'khonde. Tsopano ine ndikufuna inu mundichitire ine chinthu chimodzi. Chonde ndimvetseni ine. Mukumane ndi mtumiki wina pano ndi kukambirana ndi iwo, msonkhano ukatha. Inu muchita zimenezo? Musalole kuti zilephere. Ngati simunabatizidwepo mu ubatizo wa Chikristu, kachiteni zimenezo motsatira, ndipo kenako mukakhale ndi manja anu ali mmwamba mpaka inu mutalandira Mzimu Woyera.

²⁰⁰ Tsopano, ndipo anthu ambiri ali ndi makadi apemphero pano. Ife tiwafunsa iwo kuti ayime, ndipo abwere kuno, ndipo ine ndikuganiza muyende chodutsa. Kapena ine ndikuyenera kubwera. . . [M'bale akuti, "Ayi."—Mkonzi]. Ine sindikwanitsa kutero. ["Zibwerani kuchokera mbali iyi cha apa."] Kuchokera mbali *iyi* cha apa, akhoza kutulukira njira iyi, cha mbali iyi, anthu amene ali ndi makadi apemphero.

²⁰¹ Ndipo tsopano ngati pali aliyense wa inu amene akuyenera kupita, ndi. . . Ndachedwa. Ine ndikupepesa. Ine ndiyesetsa kuti ndidzachte bwinoko pang'ono mawa usiku. Pa. . . ndi maminiti teni kudutsa teni, mwa wotchi pakhomapo. Zikomo kwambiri chifukwa cha kupezeka kwanu usikuuno, ndipo mulole Mulungu wa Kumwamba akudalitseni inu. Ngati mukufuna kuti mukhale ndi kuwonerera mzere wa pemphero, ndinu olandiridwa nthawizonse. Koma ife tiyamba kupempherera odwala tsopano, ndipo ine sindikufuna kukugwirani inu pokhapokha ngati inu mukufuna kutsalira. Inu mwabalalitsidwa mu Dzina la Ambuye Yesu. Mulole mtendere wa Mulungu upite nanu ndi kukudalitsani inu, ndipo ukupatseni mpumulo mmatupi anu, usiku wonse, ndipo ukupatseni inu thanzi labwino kuti mudzabwerenso mawa usiku. Mulungu akhale nanu tsopano.

²⁰² Ndipo mulole iwo amene ali ndi makadi apemphero ayime chifukwa cha pemphero tsopano, pamene konsekonse tikupempherera anthu. Tsopano ife tikufuna kuti inu mudziwe, tsopano, inu amene mwaima ndi khadi la pemphero, kodi pali kukaikira kulikonse mmoyo wanu? Kodi alipo aliyense, ndikhululukireni ine, tchimo lililonse mmoyo wanu limene simunalape? Ngati liripo, ndiroleni ine ndikufunseni inu ichi. Musabwere mu mzere wa pemphero ndi tchimo losalapa mu

mtima mwanu. Chifukwa, inu mukuyenera. . . Uwu ndi mkate wa ana, mwaona. Ndipo ngati inu si Mkhristu, mupereke moyo wanu kwa Khristu, mu mzere wa pemphero, kenako mubwere. Ndi za wokhulupirira. Kodi inu muchita zimenezo? Muvomerezeni Iye poyamba ngati Mpulumutsi wanu, ndipo kenako mubwere pa nsanja, kuti mudzapemphereredwe.

²⁰³ Tsopano ine ndipempherera munthu aliyense payekha; osati kungowadutsitsa iwo, monga mtundu wina wa chizolowezi. Ife tiri mu tchalitchi tsopano. Ine ndikuganiza Mlongo Wyatt watipatsa ife chifukwa choti ife tikhoza kutsalira ndi kupemphera. [M'bale akuti, "Inde, usiku wonse, bola ngati inu mukufuna."—Mkonzi]. Ife tikhoza kukhala momwe ife tikufunira kutero. Ndipo ine ndikuthokoza Mlongo Wyatt ndi antchito kuno, chifukwa chotilola ife kuchita zimenezo. Mulungu amudalitse iye. Mwamuna wake wochirimika amaima pa nsanja iyi, amapempherera odwala, mpaka iye anamwalira, monga momwe ine ndikudziwira, msirikali weniweni wa mtanda. Ndipo tsopano ine ndikuyesera kuti ndipitirize kuchita chinthu chomwecho, kudalitsa anthu awa.

²⁰⁴ Ndipo tsopano ine ndikupemphera kuti aliyense wa inu azidutsa apa. . . Simukuyenera kuvomereza chirichonse chimene inu mukufuna kutero. Inu simukusowa kuti munene chirichonse cholakwika ndi inu. Ingobwerani ndipo mudzandilole ine ndidzakupempherereni, ndipo mukhulupirire.

²⁰⁵ Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu wandituma ine kuti ndidzachite izi? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Mukukumbukira chimene Mngelo wa Ambuye ananena? "Ngati udzawapangitse anthu kuti akukhulupirire iwe, kukhala owonamtima pamene ukupemphera, palibe chimene chidzayime patsogolo pa pemphero." Ndipo inu mukudziwa kuti izo nzoona. Izo zatsimikiziridwa, mobwereza ndi mobwereza.

Tsopano ine ndifunsa kuti Mlongo wathu Rose, ngati angatero, kuti ayimbe iyo, *Kungo Khulupirira*, kapena, *Msing'anga Wamkulu Tsopano Ali Pafupi*, kapena chinachake.

²⁰⁶ Ine ndikufuna aliyense wa inu tsopano mu—mu chiyanjano ndi ine. Kodi mutero, nanunso, anthu inu amene simuli mu mzere wa pemphero, kodi inu mudziwapempherera anthu awa? Chabwino, alonjezeni iwo izo, pokweza mmwamba dzanja lanu, "Ine ndikhala ndikupemphera, mwaona. Ife tonse tikhala tikupemphera." Chabwino. Eya.

Ine ndikanafuna kuti inu, ngati inu mukuyenera kuchokapo, mupite mwakachetechete kwenikweni tsopano, kuti iwo asavutike pamene ife tikupemphera.

Kodi iwe ukukhulupirira kuti izo zitha tsopano, mlongo? [Mlongo akuti, "Ndi mtima wanga wonse."—Mkonzi].

Wokonedwa Mulungu, ine ndikuyika manja anga pa mlongo, ndikutsutsa kusawutsika kwa thupi lake. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole izi zichoke kwa iye. Amen.

Akudalitseni inu, mlongo.

Inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Machimo anu onse avomerezedwa? Ndinu, monga momwe inu mukudziwira, ndinu wokonzeka kulandira machiritso anu?

207 Wokonedwa Mulungu, ine ndikuyika manja anga pa mlongo wanga, mu Dzina la Mwana Wanu, Yesu Khristu, ndipo ndikupempha kuti kusautsika kwa thupi lake kuthe, mu Dzina la Yesu. Amen.

Machimo onse awululidwa, ndipo wakonzekera machiritso ako? Iwe ukukhulupirira, m'bale? [M'baleyo akuti, "Ndikukhulupirira ndi mtima wanga wonse."—Mkonzi].

208 Wokonedwa Mulungu, ine ndikuyika manja anga pa m'bale wanga, monga ife tikudziwira kuti Inu muli pano, Ambuye. Ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse iye, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Machimo onse awululidwa? Ayi, iwe sumamva. Iwe ukukhulupirira kuti umva? [Mlongo akuti, "Ine ndikukhulupirira. Koma ndakhala wogontha."—Mkonzi]. Iwe ukhulupirire.

Mkaziyu ndi wogontha tsopano. Ife tipemphera pano.

209 Wokonedwa Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse mlongo wathu, ndi kuchotsa kugontha uku pa iye. Iye akukhala mu dziko lotsekeka, kumene iye sangamve. Ine ndikupemphera kuti Inu mumupatse iye machiritso, kudzera mu Dzina la Yesu.

210 Ine ndiwafunsa anthu kuti mutu wanu ukhale woweramitsidwa, miniti. Ndikufuna ndiwone chimene chachitika kwa iye. Tsopano, chonde, mu Dzina la Yesu Khristu, musalole aliyense akweze mutu wake kapena maso. Tsopano, inu musachite izo mpaka ine nditakuuzani inu kuteru.

211 Kodi iwe ukundimva tsopano? [Iye akuti, "Zina zosamveka." M'bale Branham akuwombetsa manja ake kamodzi. "Ine ndikukumvani inu."—Mkonzi]. Ukundimva ine? ["Zina."] Ukukhoza kumva? Iye akukhoza kumva tsopano. [M'bale Branham akuwomba mmanja kamodzinso.] Mukuona? Wamva phokoso limenelo?

212 Tsopano iwe ukhulupirire ndi mtima wako wonse. Iwe utero? Ndipo iwe ukhulupirire, ndipo Mulungu akuchiza kwathunthu. Iye anatero. Ine ndinangopemphera ndi kuika manja anga pa makutu ake, ndipo iye akuti akukhoza kumva chinachake. Chabwino, zingopitirira tsopano, ukukhulupirira kuti umva mwangwiro, ndipo iwe umva.

Kodi machimo onse avomerezedwa, mlongo? [Mlongo akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Kodi wakonzekera machiritso ako? [“Inde.”]

213 Wokonedwa Mulungu, ine ndikuyika manja anga pa mlongo wanga, podziwa kuti mwa ife mulibe chinthu chabwino, mwa ifeeni. Koma ife tikudziwa kuti ndife Akhristu, obadwa mwa Mzimu wa Mulungu. Ndipo ife tikuyika manja pa mlongo wathu ndi kupempha machiritso ake, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

214 Tsopano iwe ukukhulupirira kuti uchiritsidwa? [Mlongo akuti, “Zabwino.”—Mkonzi]. Chabwino, tsopano iwe—wachiritsidwa. Ndiyo njira yochitira izo. Uko nkulondola. Kulondola.

215 Machimo onse avomerezedwa? [Mlongo akuti, “Inde, bwana.”—Mkonzi]. Ndipo iwe wakonzekera machiritso ako? [“Inde.”] Iwe ukukhulupirira, posanjika kwa manja, kuti Mulungu Amene amadziwa mitima ya anthu, akuchiza iwe? [“Ine ndikutero.”]

216 Atate athu Akumwamba, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse mlongo wathu, pamene ife tikuika manja athu pa iye ndi kupempha mu Dzina la Yesu Khristu kuti Inu mumuchiritse iye. Amen.

217 Iwe uli bwanji? Ndithudi, ukudziwa kuti ndikudziwa chomwe chiri cholakwika ndi iwe. Koma basi sindikunena icho; chifukwa, iwe ukudziwa, izo zi—izo zikhala zikungopitirira ndi kumapitirira. Koma ngati ungashe. . . Kodi machimo onse avomerezedwa? [Mlongo akuti, “Inde, bwana.”—Mkonzi]. Ndipo iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akuchiritisa iwe? [“Inde, bwana.”] Kodi iwe ukukhulupirira nyamakazi. . . Ndanena kale izo.

Wokonedwa Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mumuthandize iye ndi kumuchiritisa iye. Perekani izi, mu Dzina la Yesu.

Iwe sukhala wolumala. Kazipita, ukhulupirire ndi mtima wako wonse.

218 Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akuchiza? [Mlongo akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Machimo onse avomerezedwa ndipo wakonzekera machiritso ako? Iwe ukukhulupirira kuti nsana wako ukhala bwino?

Wokonedwa Atate Akumwamba, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse iye ndi kumupanga iye kukhala bwino. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole izo zikhale chomwecho. Amen.

Mulungu akudalitse iwe, mlongo. Pita, ukukhulupirira tsopano.

Kodi machimo onse avomerezedwa, mlongo, iwe wakonzekera machiritso ako?

Wokonedwa Mulungu, machimo ake, iye akuti, avomerezedwa. Ine ndikuyika manja anga pa mkazi uyu, mu Dzina la Yesu Khristu, ndikupempha machiritso ake. Ameni.

²¹⁹ Kodi machimo onse avomerezedwa? Ukuyenera kukhala wolondola, ukudwala kwambiri, ukudziwa zimenezo. Ukudziwa kuti ine ndikudziwa chimene chiri cholakwika ndi iwe. Ndipo kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akuchiza iwe, achiritsa mtima wako ndi kukupanga iwe kukhala bwino kwathunthu?

Wokonedwa Mulungu, ine ndikupemphera kuti mu Dzina la Yesu Khristu, kuti Inu mumuchiritse iye ndi kumupanga iye kukhala bwino. Mulole ichi chimusiye iye, Atate, mu Dzina la Yesu. Ameni.

Mulungu akudalitse iwe tsopano. Usakayikire. Pita, ukukhulupirira.

Machimo onse avomerezedwa? Kodi wakonzekera kuchiritsidwa?

Wokonedwa Atate Akumwamba, ine ndikuyika manja anga pa mlongo wathu. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole iye achiritsidwe. Ameni.

Usakayikire. Pita, ukukhulupirira.

Machimo onse avomerezedwa, wakonzekera kuchiritsidwa?

²²⁰ Wokonedwa Atate Akumwamba, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse m'bale wathu, mumuchiritse iye. Perekani izi, Atate. Ine ndikuyika manja anga pa iye, kwa cholinga ichi, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

Mulungu akudalitse iwe. Ine ndikukhulupirira izo ndi mtima wanga wonse.

Kodi iwe ukukhulupirira tsopano, mlongo? Machimo onse avomerezedwa ndipo wakonzekera kuchiritsidwa?

Wokonedwa Mulungu, ine ndikuyika manja anga pa mlongo, mu Dzina la Yesu Khristu, mulole iye achiritsidwe kwa ulemelero Wanu. Ameni.

²²¹ Tsopano nthawi zambiri monga choncho, kukhudza chabe, monga Yesu ananenera, “Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala.” Ine ndayamba kuzindikira, mmisonkhano, kuti izo zimachitika mwabwinoko fifite peresenti kuposa momwe izo zimachitira pamene iwe uwayitanira anthu mu mzere, kukhala ndi kuzindikira za mumtima, chifukwa iwe umangofikira kwa apang’ono okha. Ndipo, mwanjira iyi, pamakhala ambiri amene amachiritsidwa.

²²² Kodi wavomereza machimo ako onse a kusakhulupirira ndi chirichonse? Iwe ukukhulupirira tsopano kuti iwe uchiritsidwa? [Mlongo akuti, “Inde, ndi kupulumutsidwa.”—Mkonzi].

Wokodedwa Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu muchiritse mlongo wathu pamene ine ndikugwira manja ake ndi kupempha mu Dzina la Yesu Khristu machiritso ake. Amen.

Mulungu akudalitse iwe, mlongo.

Kodi ukukhulupirira tsopano? [Mlongo akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Machimo onse avomerezedwa? [“Inde.”]

Wokodedwa Mulungu, ine ndikuyika manja anga pa mlongo wathu, mu Dzina la Yesu Khristu, kwa machiritso ake. Amen.

Mulungu akudalitse iwe, mlongo.

Zikuwoneka ngati chinthu chaching’ono kwambiri, koma ndi Mulungu Amene analonjeza icho.

Machimo avomerezedwa?

Wokodedwa Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse mlongo wathu uyu. Pamene ine ndikuyika manja pa iye mu Dzina la Yesu Khristu, mulole iye apite ndi kukhala bwino. Amen.

Machimo avomerezedwa?

Wokodedwa Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu muchiritse mlongo wathu, pamene ine ndikuyika manja pa iye, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Tsopano pamene inu mukubwera ndi zimango, mulole izo zikhudze mphamvu, izo ziyamba kugwira ntchito.

Machimo avomerezedwa? [Mlongoyo akuyankha—Mkonzi.] Iwe wakonzeka.

Wokodedwa Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse iye ndi kumupanga iye kukhala bwino, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Mulungu akudalitse iwe, mlongo.

Machimo onse avomerezedwa? [Mlongo akuti, “Chirichonse.”—Mkonzi].

Wokodedwa Mulungu, pamene mkazi uyu akundiyang’ana ine mmaso, ine ndikukhulupirira izo. Ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse iye, mu Dzina la Yesu.

²²³ Ukungomubweretsa iye, sichoncho iwe, mlongo? Iwe ukungomubweretsa iye? Chabwino. Iwe ukukhulupirira, mlongo, kuti Mulungu akuchiza iwe? [Mlongo akuti, “Ine ndikukhulupirira Mulungu akhoza kundipatsa ine kupenya kenanso.”—Mkonzi]. Mulungu akudalitse iwe.

²²⁴ Atate Akumwamba, Inu nthawizonse ndinu achifundo kwa akhungu, ndi kwa osowa. Tsopano iwo awona chimene Inu mwachita usikuuno. Chotero ife tikukhulupirira, Ambuye, chizindikiro chachikulu chotsiriza ichi chikuyenda pakati pathu tsopano. Ine ndikupempha kupenya kwa mkazi wakhungu uyu kuti kubwere kwa iye, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Tsopano, udzanene kwa ife tsopano. Udzatiuze izo.

[Mlongo akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi]. Oh, inde, iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akuchiza iwe? ["Aleluya!"]

Wokonedwa Atate Akumwamba ine ndikuyika manja anga pa mlongo wathu ndi kupempha kuti Inu mumuchiritse iye, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Mulungu akudalitse iwe, mlongo. Utilore ife tidzamve momwe iwe—momwe iwe ukuchitira.

Kodi iwe ukukhulupirira, mlongo? [Mlongo akuti, "Inde ndikutero."—Mkonzi].

O Wokonedwa Atate Akumwamba, ine ndikupempherera mlongo wathu, ndikudalira kuti Inu mumuchiza iye tsopano. Ine ndikuyika manja anga pa iye, mu Dzina la Yesu Khristu.

Tsopano khulupirirani. Uko nkulondola. Uzingopita, ukukhulupirira.

Kodi iwe ukukhulupirira, m'bale? [M'baleyo akuti, "Inde."—Mkonzi]. Machimo onse avomerezedwa?

Wokonedwa Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse m'bale wathu ndi kumupanga iye kukhala bwino, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Iwe ukukhulupirira, mlongo?

²²⁵ O Mulungu, ine ndikupemphera kuti, mu Dzina la Yesu Khristu, modzichepetsa, mu kukoma ndi kufatsa kwa ora lino, mulole Mzimu Woyera umupangitse mkazi uyu kukhala wathunthu. [Mlongo akuti, "Ndipo ine ndikupemphera, kupempherera mwana wanga. Sindinamuwone iye kwa zaka twente."—Mkonzi]. Ine ndikupemphera kuti Mulungu atumize mwana wanu wamwamuna kwa inu, mlongo, wokonedwa. Mulungu akudalitseni inu.

Atate Okonedwa, ine ndikumupempherera mlongo wathu pano. Mu kukoma kwa Mzimu Woyera, mulole Iye abwere tsopano ndi kudzachiritisa mlongo wathu, mu Dzina la Yesu. Amen.

Akudalitseni inu, mlongo.

Wokonedwa Mulungu, ine ndikumupempherera m'bale wanga, pamene iye wayima apa ndipo ine ndikuyika manja pa iye, ndi kupempha machiritso ake, mu Dzina la Yesu.

Akudalitse iwe, m'bale wanga. Chabwino.

Mnyamata wamng'ono?

Wokonedwa Mulungu, ndikuyika manja pa wamng'onoyo, ine ndikumudalitsa iye mu Dzina la Yesu Khristu, chifukwa cha machiritso ake.

Iwe ukukhulupirira tsopano, mlongo? [Mlongo akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Iwe ukufuna kuti upemphereredwe nawenso?

²²⁶ Wokonedwa Mulungu, ine ndikumupempherera iye, pamene ine ndikuyika manja pa iye. Tsopano, uku ndi kutuma Kwanu, ndi chimene Inu munati tizichita, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Inu munanena zimenezo, Ambuye. Ameni.

Tsopano, Iye ananena zimenezo, sichoncho Iye? Zikuyenera kukhala mwanjira imeneyo, mlongo.

Wokonedwa Mulungu, ine ndikumupemphera kuti Inu mumuchiritse mlongo wathu ndi kumupanga iye akhale bwino, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni. Mulungu akudalitse iwe, mlongo.

Iwe wabwera ukukhulupirira, mlongo?

²²⁷ Wokonedwa Atate Akumwamba, ine ndikumupempha madalitso Anu pa mlongo wathu, tikungomvera chimene Inu munati tichite. Inu munati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala,” Inu munati, “iwo adzachira.”

²²⁸ Mundirole ine ndiyime apa mphindi yokha, kuti ndinene mu izi, kungoti ndiwalole anthu apume kamphindi, kwa mphindi yokha. Wotsutsa nthawiina anati, kwa ine, izo siziri choncho. Koma, inu mwaona, Iye anati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira.”

²²⁹ Inu munamvapo Uthenga wanga pa *Mlandu*, kumuyika Yesu pa mlandu. Mwaona, Iye anamuza Nowa, “Kunali koti ivumba mvula.” Iyo inali isanavumbepo kwa zaka handirede ndi twente, koma iyo inavumba mulimonse. Iye anamuza Abrahamu kuti adzakhala ndi mwana wamwamuna mwa Sarah. Zinali patadutsa zaka twente-faivi. Iye sananene kuti liti. Iye anati iwo adzakhala ndi mwana wamwamuna. Zaka twente-faivi zitadutsa, izo zinadzachitika. Mwaona, Iye sananene kuti liti.

²³⁰ Iye anati, “Pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa odwala. Mulungu adzawaukitsa iwo. Ngati iwo adzaika manja pa odwala, iwo adzachira.” Kodi izo ndi zimene Iye ananena? Iye sananene kuti iwo azidzalumphalumpha ndi kumachita izo pamenepo. Iye anati, “Iwo adzachira.” Mwaona, limenelo ndi lonjezo Lake. Ndi chimene ife timakhulupirira.

Bwerani, mlongo. Inu mukukhulupirira izo kukhala zoonza? [Mlongo akuti, “Inde, ndikutero.”—Mkonzi]. Ndiye palibe njira yolepheretsa kuti muchiritsidwe.

Ine ndikuyika manja anga pa mlongo, mu Dzina la Yesu Khristu, kwa machiritso ake. Ameni.

Kodi iwe ukukhulupirira, mlongo? [Mlongo akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Machimo onse avomerezedwa, ndi okonzeka?

Wokonedwa Mulungu, ine ndikuyika manja anga pa mlongo, mu kumvera ku lamulo Lanu, ndipo ndikupempha machiritso ake, mu Dzina la Yesu. Amenii.

²³¹ Ine ndikufuna inu amene mukupemphereredwa, ine ndikufuna inu mundichitire ine chifundo. Ine ndikufuna inu munene, misonkhano iyi isanathe, chimene chiti chichitike; ndipo mungowalola omvetsera, anthu enawo, awone chimene chimachitika kwenikweni. Mwinamwake mawa, tsiku lotsatira, kapena liti, inu mungoona chimene chimachitika.

²³² Kalata yanga yawonetsa kuti ndi—ndi zosiyana kwambiri kuposa kungowalola iwo kuyesa, kuyesa chikhulupiriro chawo chomwe. Chifukwa, Yesu anati, “Iwo adzaika manja pa iwo. Iwo adzaika manja pa iwo, iwo adzachira.” Tsopano mveterani chimene Iye ananena. Iye sananene kuti iwo azidzalumphalumpa ndi kumadzathamangathamanga. Iwo akhoza kumadzachita zimenezo. Koma Iye anati, “Iwo adzachira.” Kodi icho ndi chimene Iye ananena? Ichu ndi chimene Iye ananena. Ndi chimene ine ndimakhulupirira. Ndipo Iye ali pano tsopano, Mmodzi amene anati Mawu ali pano kuti awapange iwo chomwecho.

Inu mukukhulupirira, bwana? [M’bale akuti, “Amenii.”—Mkonzi].

Wokonedwa Atate Akumwamba, pa kuvomereza kwa chikhulupiriro chake ndi kukhulupirira, ine ndikuyika manja anga pa iye, mu Dzina la Yesu Khristu, kwa machiritso ake.

Wokonedwa Mulungu, ine ndikuika manja anga pa mkazi uyu, mu Dzina la Yesu Khristu, kwa machiritso ake. Chabwino.

Wokonedwa Atate, ine ndikuyika manja anga pa mkazi uyu, mu Dzina la Yesu Khristu, kwa machiritso ake. Inu munati, “Iye adzachira.”

Mwakonzekera kuchiritsidwa, mlongo?

Wokonedwa Mulungu, ine ndikuyika manja anga pa iye, mu Dzina la Yesu Khristu, kuti Inu mumuchiritse iye.

Chabwino, mlongo, wokonedwa, chirichonse chakonzekera machiritso? Chikhulupiriro chako tsopano chakwaniritsidwa, iwe ukukhulupirira kuti ukhala bwino?

²³³ Ndipo, Mulungu, ndikuyika manja anga pa iye, mu kumvera malamulo Anu, “Kwa dziko lonse, cholengedwa chirichonse.” Ine ndikuyika manja pa iye, mu Dzina la Yesu, kwa machiritso ake.

Wokonedwa Mulungu, ine ndikuyika manja anga pa m’bale wanga, mu Dzina la Yesu Khristu, kwa machiritso ake.

Wokonedwa Mulungu, ine ndikuyika manja anga pa mlongo wanga, mu Dzina la Yesu Khristu, kwa machiritso ake.

[Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] . . . akupita pansu mu kanjira. Sindinafune kukutopetsani inu. Iwe ukhala bwino ngati iwe uti ukhulupirire izo tsopano.

Wokonedwa Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse mlongo wanga, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

[Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] . . . kuti andithandize kupempherera anthu awa.

²³⁴ Tsopano ife tiri ndi mipango ina apa, ndi zina zotero, muno, zoti zipemphereredwe. Ndipo ine ndikufuna inu mupitirize kupemphera ndi ine tsopano, tsopano, timaphukusi tating'ono iti, tsopano. Ndikudziwa kuti izi zikumveka zachilendo kwa anthu kuti apempherere chinthu chaching'ono ngati ichi. Koma ngati inu mukanangobwera mu ofesi mwanga, kamodzi, ndi kudzangowona. Ngati ife tikanasunga maumboni kudutsa zaka izi, ndikuganiza simukanaunjika pa nsanja iyi, amene achiritsidwa pongotumiza nsalu zapemphero izi monga chonchi, mamillioni a iwo, kuzungulira ndi kuzungulira dziko. Tsopano, inu mukudziwa chimene icho chiri—icho chiri?

Winawake atenge mpango umenewo pamenepo wa uyo—wamng'ono uyo. . . Iwe uwudziwa mpango wako, iwe utero, m'bale? Chabwino.

²³⁵ Ndipo ndawonapo ana aang'ono, olumala akuchiritsidwa. Ndipo inu mwaona, chimene icho chiri, ndi malo olumikizirana chabe, monga Oral Roberts anakonda kunena. Ndi malo olumikizirana chabe. Ife timapemphera. Tsopano, ife sitimachita ichi tokha, ife timachita ichi chifukwa Baibulo limatilamula ife kuti tichite ichi. Ife tonse tikudziwa kuti izo nzoona.

²³⁶ Tsopano, pali anthu ambiri amene iwo amayidzoza mipango, ndi zina zotero. Chabwino, tsopano, ife tikuganiza kuti izo nzabwino, ndithudi, koma ngati ife basi. . . Baibulo silinanene kuti iwo “anadzoza” mipango.

²³⁷ “Koma anatenga kuchokera pa thupi la Paulo mipango.” Tsopano mukuona chimene ine ndimachikamba? Tsopano, chimene iwo anachiwona, mphamvu yofulumizitsa ija imene inali mwa Paulo, kuti iwo ankadziwa kuti iye anali wantchito wa Mulungu. Iwo anadziwa kuti Mulungu anali mwa iye. Iwo anadziwa kuti chirichonse chimene iye anachikhudza chinali chodalitsidwa. Ndi angati akumvetsa zimenezo? Nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi].

²³⁸ Inu mukudziwa, ine ndikuganiza Paulo anali kwenikweni Mwamalemba mu chimene iye anachita. Kodi inu mukuganiza choncho? Inu mukufuna ndikuuzeni inu kumene ine ndikuganiza kuti iye anatenga ganizo lochita chimenecho? [Wina akuti, “Kuchokera kwa Elisha.”—Mkonzi]. Kuchokera kwa Elisha, nzoona. Mwaona, Eliya anati, “Tenga ndodo iyi ndipo upite ukaiyike iyo pa mwanayo.” Ndipo mneneriyo anatomiza ndodo chifukwa iye ankadziwa kuti chirichonse chimene iye

anachikhudza chinali chodalitsidwa. Iye ankadziwa malo ake. Iye. . . ngati iye akanangomupangitsa mkaziyo kukhulupirira chinthu chomwecho.

Tsopano mwaona, tsopano, Baibulo silinanene nkomwe, “Iwo adzapempherera odwala.” Ilo linati, “Iwo adzayika manja pa odwala.”

²³⁹ Tsopano tangoganizani, anthuwo anawona, mwa mtumwi Petro, Kukhalapo kwa Mulungu kukuwonetseredwa mwa munthu uyu, kotero kuti iwo—iwo anawaika anthu mu mthunzi wake, ndipo iwo anachiritsidwa. Ndi angati akudziwa kuti izo ndi Mwamalemba? Ndizo basi mochuluka Lemba monga Yohane 3:16. Mwaona, Iwo onse ndi Mawu a Mulungu. Tsopano, anthu, inu mukudziwa kuti mthunzi wa munthu ameneyo sunawachiritse anthu.

²⁴⁰ Koma, taonani, ngati mphamvu ya Mulungu inali pa mneneri ameneyo, kwa zaka ndi zaka iye atafa, kotero kuti munthu wakufa anaponyedwa pa thupi lake, mafupa ake. Thupilo panalibepo nkomwe; mafupa anali pamenepo. Ndipo Kukhalapo kwa Mulungu kunali pa mafupa amenewo, mpaka munthu wakufayo anakhala wamoyo.

²⁴¹ Tsopano kodi inu simukudziwa kuti Mulungu yemweyo amene anachita zinthu zonsezo ali pomwe pano usikuuno? Kwa—kwa ine, ine ndikuganiza kuti tikuyenera kukhala anthu osangalala kwambiri padziko lonse lapansi. Tangoganizani za ichi.

²⁴² Ine—ndikukhulupirira kuti sindinasangalatse omvera anga kuti akhulupirire kuti ndi chinachake chimene ndimachita inemwini. Inu—inukudziwa bwinoko kuposa izo. Ine, ine ndi m’bale wanu, mwaona, ndipo ine ndangokhala m’bale wanu basi.

²⁴³ Koma ine ndikudziwa, ine ndikudziwa ichi, kuti Mulungu ali pano. Ndipo ndikudziwa kuti Iye wapereka chinachake kwa ife, chimene ife sitingathe kuchifotozoza icho, kokha mwa Mawu a Mulungu, amati icho chikuyenera kukhala pano pa nthawi ino. Chotero, zimatipatsanso ife chizindikiritso chodziwa kuti tikukhala mmasiku otsiriza. Izo zimatipatsa ife chizindikiritso kudziwa kuti anthu awa, osankhidwa awa, osankhidwa, oyitanidwa atuluke, odziwidwiratu. . .

²⁴⁴ Tsopano, awo ndi mawu aakulu, *kudziwidwiratu*, koma ife tonse tikudziwa kuti izo ndi zooni. Ife mwamtheradi tikudziwa kuti Mulungu wopandalire anadziwiratu zinthu zonse mwa kudziwiratu maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, ngakhale Mwanawankhosa anaphedwa; ndi dzina lililonse limene lidzakhale mu Bukhu, linaikidwa pa Bukhu Bukhulo lisanalembedwe nkomwe. Tsopano ndi angati akudziwa kuti izo ndi zooni?

²⁴⁵ Ndipo Yesu anadza kuti—kuti adzawawombole iwo amene anali mu Bukhulo. Mu Baibulo, Mwanawankhosa anabwera

kuchokera kuseri kwa chophimba, ndipo anadzatenga Bukhu ndipo anatsegula Zisindikizo zimene Ilo linasindikizidwa nalo, pakuti Iye anabwera kudzatenga onse amene Iye anawawombola. Iye ndi Wopembedzera tsopano, Wopembedzera akupanga kupembedzera kwa iwo amene Iye anawawombola. Onse amene dzina lawo linalembedwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, awomboledwa.

²⁴⁶ Pamene ine ndinapanga neno lakhambi usiku wina . . . ine ndikudikirira . . . mipango yonseyi apa. Ine sindikungoyesera kuti ndilalikirensa kachiwiri, koma ndinanena kuti pali neno lapang'ono . . . Ine ndikuyembekeza izi sizikumveka mosinjirira, mwaona. Koma monga mlimi amene anaika nkhu, ndipo analibe mazira okwanira, chotero iye anatenga dzira la mphungu, ndipo anadzaliika ilo pansi pa nkhu ndipo iyo inaswa mphungu. Ndipo iyo inali yosamvetseka kwambiri pakati pa nkhu zonse, chifukwa izo sizinkawona zinthu mofanana. Koma ndizo zonse zimene iyo inayamba yaziwonapo, inali nkhu. Iyo inkangomva liwu limodzi lokha, silimamveka ngati liwu lake. Komanso iyo sikanatha kuyankhula ngati nkhu yaikazi kapena nkhu. Iyo sinayamikire chakudya chawo, pamene izo zinkadya kuchokera mu khola. Panali chinachake chosiyana ndi iyo, komabe iyo sinkadziwa chomwe chinali kusiyana kwake.

²⁴⁷ Ndipo kenako tsiku lina, apo panali mayi mphungu amene ankadziwa kuti iye anali ataikira mazira ochuluka kwambiri. Ndipo panali limodzi la mazira amenewo, limene linali loti likhale mwana wake, linasowa. Chotero iye anapita kukasakasaka iye, ndipo iye anamupeza iye mu khola. Ndipo iye anakuwana. Ndipo pamene iye anafuula, kamphungu kakang'ono kanadziwa liwu la amayi ake. Monga Yesu ananena, “Nkhosa Zanga zimadziwa Liwu Langa.”

²⁴⁸ Ine ndikuganiza, usiku wathawu, pamene ine ndinawona gulu lija la Abaptisti, Apresbateria, ndi ena otero, iwo akhoza kukhala kuti anatulutsidwa pansi pa nkhu. Mundikhululukire ine, m'bale, mwaona. Koma Amayi ankadziwa kuti Iwo anali ndi okondedwa Ake kunja uko kwinakwake. Chotero amuna amenewo atayima pamenepo, osatsutsa kudya kumene iwo analandira kuchokera kwa mayi wa nkhu, ndi zina zotero, koma tsopano izo ndi mphungu, inu mwaona, izo zimaulukira chakudya chawo. Mukuona?

²⁴⁹ Ndipo ine ndikuganiza mpingo ndi chinachake chonga chochitika chimene ine ndinachiwona osati kale, ndikubwera kuchokera ku Tucson, kapena kuchokera—kuchokera ku Phoenix, kupita ku Tucson. Ine ndinaona chodabwitsa. Ndipo chinangondiswa mtima, kuwona chimene chinachitikacho, momwe . . . khwangwala, amene ankauluka mu mlengalenga, mchimwene wa mphungu, chimene chiri choimira cha mpingo.

Ndipo Yehova ndi Mphungu. Iye anawatcha aneneri Ake “mphungu.” Iye anadzitcha Yekha, Yehova, “Mphungu.”

²⁵⁰ Koma khwangwala uyu wataya chomuzindikiritsa chake, chifukwa sakumawulukanso mu mlengalenga ndi kukasaka nyama yake monga momwe amayenera kuchitira. Koma iye amakhala pa mawaya a telefoni ndi kumachita ngati khungubwe. Iye—iye amakasaka akalulu akufa amene magalimoto awapha, ndipo iye ndi mphamba amatuluka kunja kumeneko ndi kumakadyera limodzi. Iye amadumphana ngati mphamba, mmalo moyenda mmene akuyenera kuyendera. Iye wataya chomuzindikiritsa chake.

²⁵¹ Ndipo ine ndikunena ichi ndi chikondi chonse chaumulungu ndi ulemu, mpingo wataya kale chochizindikiritsa chake ngati mphungu yachibale. Iwo umakhala mozungulira. Mmalo mokumba mu Mawu ndi kufufuza ngati zinthu izi ziri zolondola, iwo umayembekezera mulu wa zolemba za Sande sukulu zimene zapangidwa ndi gulu la aluntha kwinakwake, kalulu wina wakufa amene anaphedwa kwinakwake. Umalumpha ngati mphamba! Mulungu atithandize ife kuwulukira kutali kwa izo.

Malonjezo awa ndi owona. Osati chimene winawake ananena za Iwo, koma chimene Mulungu ananena za iwo! Iwo ndi owona. Ndine wokondwa kukhala oyanjana ndi mphungu.

Tiyeni tipemphere limodzi chifukwa cha odwala athu.

²⁵² Okonedwa Atate Akumwamba, zinaphunzitsidwa mu Baibulo kuti iwo anatenga kuchokera mu thupi la Paulo, mipango ndi zovala, ndipo ziwanda zinatuluka mwa anthuwo, ndipo mizimu yonyansa inatuluka mwa iwo. Tsopano, Atate, ine ndaima apa pa mipango iyi, ikuyimira munthu aliyense amene alipo. Ndi Thupi la Khristu, ife pamodzi. Ife tikudzinenera, mwa chisomo ndi chikondi, kuti ife tiri pano kuti tiyimire Mkwatibwi Wake, ndi kukhulupirira, kuyanjana ndi Iye mu Ufumu Wake. Ndipo ife tikudziwa kuti sitiri Paulo Woyera, koma ife tikudziwa Inu mukadali Yesu.

²⁵³ Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mulemekeze chikhulupiriro cha anthu awa. Ngati iwo akanakhala moyo mmbuyo mu masiku a Paulo, iwo akanamva Uthenga womwewu, akanawona zinthu zomwezi. Chifukwa chake, iwo ndi anthu amtundu womwewo. Inu ndinu Mulungu yemweyo. Chotero ine ndikupemphera, Wokonedwa Mulungu, kuti Inu mulemekeze chikhulupiriro chawo, monga Inu munachitira izo mmasiku a Baibulo. Ndipo mulole mphamvu iliyonse ya chiwanda, nthenda iliyonse, kusautsika kulikonse, zomwe zawamanga anthu omwe mipango iyi ndi maphukusi apa zikuyimira, mulole mphamvu yoyipa ya matenda iwachokere iwo.


²⁵⁴ Zinanenedwapo, nthawi ina, kuti Israeli ankayenda mu mzere wa ntchito, akupita ku dziko lolonjedwa. Ndipo pomwepo mu mzere wa ntchito, mdani anabwerapo ndipo

anadzawayika iwo pa ngodya, ndipo Nyanja Yofiira inawadula iwo pa mzere wa ntchito, ndiponso mu kuguba kwawo. Ndipo Mulungu anayang'ana pansi kuchokera mmiyamba, kudzera mu Lawi la Moto, ndipo nyanja inachita mantha. Iyo inadziyalula mafunde ake, chifukwa mafunde a Mulungu anali pansi pa nyanja. Ndipo Ilo linapanga njira kwa ana Ake, akuyenda mu mzere wa kumvera.

²⁵⁵ Tsopano, Mulungu, ngati Nyanja Yofiira ingachite mantha, ndi kugudubuzira mmbuyo mafunde ake, kugudubuzira mmbuyo madzi ake, ndi kupereka malo kwa ana apaulendo akuyenda momvera; Wokondedwa Mulungu, usikuuno, muyang'ane pansi kudzera mu Magazi a Mwana Wanu, Yesu, Amene anapanga lonjezo. Ndipo pamene mipango iyi ikaikidwa pa matupi a anthu odwala, mulole maso a Mulungu akayang'ane, ndipo mulole matenda amenewo, mdierekezi ameneyo, akawopsyzedwe ndipo akasunthire kutali. Ndipo mulole anthu asunge ulendo wopita ku Dziko lolonjezedwa, ali ndi thanzi labwino ndi amphamvu. Pamene Israeli ankaguba kudutsa mchikululu, panalibe munthu mmodzi wofooka pakati pawo, ku mapeto enawo. Mulole izo ziperekedwe kwa anthu awa, Atate, pakuti ife tikutumiza mipango iyi, mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii.

²⁵⁶ Mulungu akudalitseni inu, aliyense. Pamene inu mukudzatenga mipango yanu tsopano, inu mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu amamva izi? Mukuona? Ine—ine ndikufuna kunena ichi. Musati, musakayikire, mpang'ono pomwe. Mwaona, izo zikhoza kuwoneka zachirendo kwenikweni. Mundikhululukire ine, miniti yokha. Musakayikire, mpang'ono pomwe. Koma mukhulupirire tsopano kuti, zimene ife tapempha, Mulungu apereka.

²⁵⁷ Kodi inu mukukhulupirira kuti ameneyo ndi Mulungu apa, akudziwa chinsinsi cha mtima wanu? Inu mukudziwa ndi kukhulupirira ameneyo ndi Mulungu? Tsopano ingokhazikitsani malingaliro anu tsopano, izo sizingakhale china chirichonse. Mukuona?

²⁵⁸ Tsopano, bwanji ngati pakanakhala mawa lalikulu, zaka zapitazo iyi ingakhale mbiriyakale. Ndipo pamene anthu, mu zaka ziri nkudza, ngati izo zikanati zidzakhale moteromo, iwo angabwere ndi kudzati, “Chabwino, ngati ine ndikanakhala ndi moyo nthawi imeneyo, ine ndikanaziwona izo zikuchitika, mnyamata, ndizo zonse zimene ine ndikanayenera kuti ndidziwe. Ine ndikanakhulupirira izo pamenepo!” Mwaona, chinthu chomwecho chimene mukukhulupirira, ngati inu mukanakhala kumbuyo uko pamene Iye ankachita izo apo! Kumbukirani, akadali Iyeyo. Ndi Moyo Wake mwa inu. Mulungu akudalitseni. 

65-0426 Kutsimikizira Mawu Ake
Embassy Hotel
Los Angeles, California U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org